



Nzeru Ya Mulungu

Adrian Ebens

Nzeru ya Mulungu

Chiyambi cha Mukangano Waukulu

Wolembe: Adrian Ebens

Otsindikidza :



Lolembedwa mundondomeko ya nkhani, March, 2010

Kutsindikizidwa February, 2016

Kukonzedwaso April, 2018

Zamkati :

1. Atate Athu	5
2. Olamulira zonse.....	8
3. Nzeru ya Mulungu	11
4. Chifanano	15
5. Chifuniro.....	18
6.Vuto liyamba	19
7. Kulengedwa muchifanizo chake	23
8. Tate wa Mabodza	27
9. Kukopeka kwa anthu	29
10. Mwachidule.....	33
11. Njira ziwiri.....	34
12. Chiyambi cha Babulo	36
13. Zochitika mu Babulo.....	40
14. Njira ya Mibadwo	44
15. Kuyitanidwa kutuluka mu Babulo.....	48

1. Atate Athu

Pamene om'tsatira ake atamuwandikira Yesu tsiku lina, adampepha iye chinthu chofunikira kwambiri:

Luka 11:1 Ndipo kunali, pakukhala iye pamalo pena ndi kupemphera, m'mene analeka, wina wa ophunzira ace anati kwa iye, Ambuye, tiphunzitseni ife kupemphera, monganso Yohane anaphunzitsa ophunzira ace.

Yakho lomwe Yesu anapereka likuti iye chinthu chofunikira kwambiri kuti tidziwe za Mulungu. Ntchito yapemphero ndiyofuna kulankhulana ndi kulumikidzana ndi Mulungu. Dzina lomwe Yesu anagwiritsa ntchito koyamba ndi chizindikiro chomwe Mulungu aliri. Umu ndimomwe Yesu anaphunzitsira pamene tifuna kulankhulana ndi Mulungu mupemphero:

Luka 11:2 Ndipo anati kwa iwo, M'mene mupemphera nenani, Atate, Dzina lanu liyeretsedwe, Ufumu wanu udze.

Atate athu. Kupatura zonse zomwe tingamuyerekedzere Mulungu, Mulungu ndi oyamba ndipo chachikulu ndichoti Iye ndi Atate. Kufotokonzera kochepeko kukutiwudza ife zambiri zonkhudzana ndi Mulungu. Zikutiwudza ife kuti padzonse Mulungu ndiye wa ubale. Akufuna ife poyankhulana naye tiyankhulane mwa ubale. Mawu woti Atate sali wonena kokha zakuthekera ndi mphamvu, koma zikuyakhula za ubale ndi kulumikizana ndi chirengedwe. Ndi Atate, komanso chiyambi cha zonse. Nanga ndi Atate otani Mulungu?

Mose tsiku lina adamfutsa Mulungu kuti amuwulurire ulemerero wake, kapena chomwe chiri chofunikira kwambiri cha Mulungu. Umu ndi momwe Mulungu adayakhira:

Eksodo 34:5,6 Ndipo Yehova anatsika mumtambo, naimapo pamodzi ndi iye, napfuula dzina la Yehova. Ndipo Yehova anapita pamaso pace, napfuula, Yehova, Yehova, Mulungu wachifundo ndi wacisomo, wolekerezwa, ndi wa ukoma mtima woculuka, ndi wacoonadi.

Onani momwe Mulungu adamuwonetsera Mose. Adamuwudza iye za khalidwe lake. Ichi ndi chinthu cha ulemerero waukulu wa Mulungu - khalidwe lake. Iye ndiwachifundo, chisoni, ofatsa, odzala ndi zabwino ndi choonadi. Mudziko lomwe tikhukhalari zikhaliidwezi ndi zochepe, koma pamene tikuyetsera kukwaniritsa zinazi, ambiri a ife timayamikira kwambiri. Mtumiki Yohani anatsokhanitsa za khalidwe la Mulungu pomwe anati:

1 Yohane 4:8 iye wosakonda sazindikira Mulungu; cifukwa Mulungu ndiye cikondi.

Mulungu ndi Atate wachikondi yemwe asamala kwambiri chirengedwa chake. Nanga chirengedwe chake ndichachikulu bwanji?

Buku lopatulika (Baibulo) limatiwudza ife kuti Mulungu ndiye Atate wazonse zakumwamba ndi za dziko lapansi.

Aefeso 3:14,15 Cifukwa ca ici ndipinda maondo anga kwa Atate, amene kucokera kwa Iye fuko lonse la m'mwamba ndi la pa dziko alitcha dzina.

Chirengedwe chonse chiri m'manja mwa Atate athu a kumwamba, ndipo yese amene ali mu chirengedwechi ali chiwala cha banja lake. Pali ambiri mwa ife omwe tikhoza kuyesedwa kuti Mulungu sangaganizire aliyese, ndipo ena kuyiwalidwa kumene, koma mvetserani modekha momwe Yesu anafotokozera za izi:

Luka 12:6,7 Kodi mpheta zisanu sizigulidwa timakobiri tiwiri? ndipo palibe imodzi ya izo iiwalika pamanso pa Mulungu; komatu ngakhale matsitsi onse a pamutu panu amawerengedwa. Musaopa, muposa mtengo wace wa mpheta zambiri.

Mulungu sayiwala aliyense. Amadziwa zambiri za ife ndipo ali wachidwi ndi miyoyo yathu ndi zomwe tichita ndi maganizo athu. Komabe samasiya kutiganizira ife.

Masalimo 40:5 Inu, Yehova, Mulungu wanga, zodabwitsa zanu mudazicita nzambiri, ndipo zolingirira zanu za pa ife; palibe wina wozifotokozera Inu; ndikazisimba ndi kuzitchula, zindiculukira kuziwerenga.

Ali ndi malingaliro apadera ndi ife komaso ndi loto lomwe tingakhalire.

Yeremiya 29:11 Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezere.

Chiri chonse chabwino tiri nacho chinachokera kwa Iye.

Yakobo 1:17 Mphatso iri yose yabwino, ndi chininkho ciri conse cangwiwo zicokera Kumwamba, zotsika kwa Atate wa mauniko, amene alibe cisanduliko, kapena mthunzi wa citembenukiro.

Chionetsero chodabwitsa kwambiri chimene anaonetsa m'mene Mulungu amaganizira ife ndi pamene anayankhula pa ubatizo wa Mwana wake yekha - Yesu. Umu ndi momwe anayakhulira:

Mateyo 3:17 ndipo onani, mau akucokera kumiyamba akuti, Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera.

Mulungu anakonda Mwana wake ngati munthu. Anali wotsangalala ndi Iye. Chachikulu pa ichi ndi kudzindikira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Ifenso tikhodza kulandiridwa motero.

Aefeso 1:6 kuti uyamikidwe ulemerero wa cisomo cace, cimene anaticitira ife kwaufulu mwa Wokondedwayo.

Tikhala tikufufudza zambiri za ntchito ya Yesu komanso chifukwa chomwe adabwerera ku dziko lapansi ndi chifukwa chomwe ife tiyenera kulandiridwa kupyolera mwa Iye. Koma chimene tifuna kutsindika apa ndichoti Mulungu ndi wachikondi ndi wotitsamalira ife ndipo ali ndi chidwi ndi china chirichonse cha moyo wathu.

2. Olamulira zonse

Mutu wambuyomu tinadzindikira kuti Mulungu ndi Atate wachikondi yemwe amaganizira za ife pafupipafupi, ali ndi cholinga ndi loto padza tsogolo lathu. Tinadzindikira kuti ndi Atate wa chirengedwe chonse. Mundime iyi, tikufuna tiwone zikhumbo zolora Mulungu kukhala ndi kupanga zithu zomwe amachita.

Choyamba Baibulo limatiwudza ife kuti Mulungu ndi Ambuye ndiponso Wolamulira wa chiri chonse.

1 Akorinto 8:6 koma kwa ife kuli Mulungu mmodzi, Atate amene zinthu zonse zicokera

1 Timoteo 1:17 Ndipo kwa Mfumu yotsatha, yosavunda, yosaoneka, Mulungu wa yekha, ukhale ulemu ndi ulumerero, kufikira nthawi za nthawi. Amen.

Deuteronomo 6:4 Imvani, Israele; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi;

Atate ndiyekhayo Mulungu komwe zonse zimachokera. Mulungu sanalandire mphamvu yake, nzeru kapena chidziwitso kuchokera kwa wina wake. Zonse tikudziwonazi zinachokera kwa iye.

Yesaya 40:10-15 Taonani, Ambuye Yehova adzadza ngati wamphamvu, ndipo mkono wake udzalamulira; taonani, mphoto yake iri ndi Iye, ndipo cobwezera cace ciri patsogolo pa Iye. Iye adzadyetsa zoweta zace ngati mbusa, nadzasonkhanitsa ana a nkhosa pacapa pace, nadzawatengera pa cifuwa cace, ndipo adzatsogolera bwinobwino zimene ziyamwitsa. Ndani wayetsa madzi m'dzanja lace, nayesa thambo ndi cikhato, ndi kudzaza pfumbi la nthaka m'nsengwa, ndi kuyesa mapiri m'mbale zoyesera, ndi zitunda m'mulingo? Ndani anapangira mzimu wa Yehova, kapena kukhala phungu lace, ndi kumphunzitsa Iye? Iye anakhala upo ndi yani, ndipo ndani analangiza Iye ndi kumphunzitsa m'njira ya ciweruzo, ndi kumphunzitsa nzeru ndi kumuonetsa njira ya luntha? Taonani, amitundu akunga dontho la m'mtsuko, nawerengedwa ngati pfumbi losalala la m'muyeso; taonani atukula zisumbu ngati kanthu kakang'ono.

Masalimo 36:7-9 Ha! cifundo canu, Mulungu, ncokonedwadi! Ndipo ana a anthu athawira kumthunzi wa mapiko anu. Adzakhuta kwambiri ndi zonona za m'nyumba mwanu, ndipo mudzawamwetsa mumtsinje

wa zokondweretsa zanu. Pakuti citsime ca moyo ciri ndi Inu, M'kuunika kwanu tidzaona kuunika.

Mulungu ndi mphamvu zonse, kutanthauza kuti mphamvu ya Mulungu iribe malire; ndiyopanda malekezero. Mphamvu yake ndiyopambana kwambiri. Mphamvu yake yosamvetsetseka mumafotokozeredwe. Ndidzobvuta kumuphunzitsa Iye chifukwa chidziwitso chake ndi chosasimbika, timatcha ichi wodziwa zonse. Nzeru zonse ndi chidziwitso chonse zimachokera kwa Iye.

Mphamvu ndi nzeru izi zimasefukira mwa ife kupyolera mu Mzimu wake omwe ulingati mtsinje.

Chivumbulutsa 22:1 Ndipo anandionetsa mtsinje wa madzi a moyo, wonyezimira ngati krustalo, oturuka kumpando wachifumu wa Mulungu ndi wa Mwana wa nkhusa.

Masalimo 46:4, 5 Pali mtsinje, ngalande zace zidzakondweretsa mudzi wa Mulungu. Malo oyera okhalamo Wam'mwambamwamba. Mulungu ali m'kati mwace, sudzasunthika, Mulungu adzauthandiza mbanda kucha.

Kudzera Mzimu wake Mulungu akhoza kukhala paliponse pa nthawi yimodzi. Ichi chimatchedwa kuti akupezeka ponseponse. Komanso ndi zithu zomwe ndidzobvuta kudzimvetsa, koma mverani zomwe Baibulo likulakhura:

Masalimo 139:7-10 Ndidzapita kuti kuzembera mzimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kudzembera nkhope yanu? Ndikakwera kumka kumwamba, muli komweko; Kapena ndikadziyalira ku Gehena, taonani, muli komweko. Ndikadzitengera mapiko a mbanda kucha, ndi kukhala ku malekezero a nyanja; Kungakhale komweko dzanja lanu lidzanditsogolera, Nilidzandigwira dzanja lanu lamanja.

Mtsinje uwu ndi mtsinje wa moyo, zonse zothandizira moyo zimachokera ku Mzimu ndipo ndi Moyo wake - kupereka Mzimu mwa ife kutisunga ndi moyo ndi mitima yathu kupuma.

Machitidwe 17:24-28 Mulungu amene analenga dziko lapansi ndi zonse ziri momwemo, Iyeyo, ndiye mwini kumwamba ndi dziko lapansi, sakhala m'nyumba za kachisi zomangidwa ndi manja; satumikilidwa ndi manja a anthu, monga wosowa kanthu, popeza Iye mwini apatsa zonse moyo ndi mpweya ndi zithu zonse; ndipo ndi mmodzi analenga mitundu yonse ya anthu, kuti akhale ponse pa nkhope

ya dziko lapansi, atapangiratu nyengo zao, ndi malekezere a pokhala pao; kuti afunefune Mulungu, kapena akamfufuze ndi kumpeza, ngakhale sakhala patali ndi yense wa ife; pakuti mwa Iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu; monga enanso a akuimba anu ati, ‘Pakuti ifenso tiri mbadwa zake’.

Ndiye machidule tikuwona kuti Mulungu alipo yekha yemwe ndi wamphamvu, odziwa ndiwopedzeka palipose mu Mzimu wake. Lamulo lonse ndi mphamvu zimachokera kwa iye ndiye amapereka kulikonse.

3. Nzeru ya Mulungu

Zikhoza kubwera modzidzimusa kuganiza kuti monga wamphamvu zonse ndi nzeru zonse ali mu udindo oti Iye sakanatha kuchita china chake. China chake chofunika kwambiri choti chopanda icho, Mulungu Atate sakanatha kukhazikisa Ufumu Wake.

Tikati tiwonetsetse modzama pafundo yoti moyo wonse ndi nzeru zonse, zichokera kwa Mulungu, tidzindikira kuti Mulungu sakadalenge zonse zikupedzeka mu chirengedwe chake, ndi kupereka mundanda wa zoti azitsatire. Khalidwe logonjera kwa Mulungu, kukhulupirira Iye, ndikusunga Njira Yake yopangira zinthu zonse yinayenera kukhala mbali ya Mtsinje wochokera ku mpando wa Mulungu.

Bvuto ndiroti Mulungu sachitira kwa wina, kapena kumvera wina kapena kutsatira njira zawo zochitira zithu, choncho Iye sapereka zithu ngati izi. Mu nzeru yopambana, Mulungu adatumiza Mwana wa Iye yekha muchifaniziro chake, kupereka kwa Iye zonse alinazo ndi kulenga zonse kuchokera mwa Iye. Dziwani:

Ahebri 1:1-5 Kale Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiya-siyana, koma pakutha pace pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe: ameneyo, pokhala ali cinyezimiro ca ulemerero wace, ndi cizindikilo ceni ceni ca cikhalidwe cace, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yace, m'mene adacita ciyeretso ca zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'Mwamba, atakhala wakuposa angelo, monga momwe adalowa dzina lakuposa iwo. Pakuti kwa mngelo uti anati nthawi iri yonse, Iwe ndiwe Mwana wanga, Lero Ine ndakubala Iwe? ndiponso, Ine ndidzakhala kwa iye Atate, Ndipo Iye adzakhala kwa Ine Mwana?

Yohane 5:26 Pakuti monga Atate ali ndi moyo mwa Iye yekha, momwemonso anapatsa kwa Mwana kukhala ndi moyo mwa Iye yekha;

Yohane 5:19 Pamenepo Yesu anayankha nati kwa iwo, Indetu, indetu ndinena kwa inu, sakhoza Mwana kucita kanthu pa yekha, koma cimene aona Atate acicita, ndico. Pakuti zimene Iye azicita, zomwezo Mwananso azicita momwemo.

Yohane 8:29 Ndipo wondituma Ine ali ndi Ine: sanandisiye Iye pa ndekha; cifukwa ndicita Ine zimene zimkondweletsa Iye nthawi zonse.

Yohane 8:42 Yesu anati kwa iwo, Mulungu akadakhala Atate wanu, mukadakhala Ine; pakuti Ine ndinatuluka, ndi kucokera kwa Mulungu; pakuti sindinadza kwa Ine ndekha, koma Iyeyu anandituma Ine.

Akolose 2:8-10 Penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati cuma, mwa kukonda nzeru kwace, ndi cinyengo copanda pace, potsata mwambo wa anthu, potsata zoyamba za dziko lapansi, osati potsata Kristu; pakuti mwa Iye cikhalaria cidzalo ca Umulungu m'thupi, ndipo muli odzazidwa mwa Iye ndiye mutu wa ukulu wonse ndi ulamuliro;

Indedi zonse zofunikira ku chirengedwe chonse cha Mulungu tsopano zikhala mwa Mwana wake; mphamvu, nzeru, moyo, komanso kudalira ndi kumvera, kuzindikira ulamuliro wa Mulungu ndi malingaliro a chikondi cha Mulungu ndi kulandiridwa. Mwana wa Mulungu ndi kukwanira kwa Mulungu mwini ndichiyambi chamadziko a Ufumu wa Mulungu.

Afilipi 2:9-11 Mwa ichinso Mulungu anamkwezetsa Iye, anampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansu pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate.

Ndiye Atate anamukweza Mwana wake ndikumupanga Iye wa mphamvu ya umulungu yonse ndi kukhala chitsanzo ku chirengedwe chonse. Mulungu amatumiza Mzimu wa Mwana wake ku moyo wa zolengedwa zonse kuzipatsa moyo, malingaliro a m'dalitso ndi kudziwa kugonjera ndi kukhulupirira kumvera. Popanda Mzimu wa Kristu nkovuta kudziwa kugonjera, kukhulupirira ndi kumvera Mulungu. Onani momwe Baibulo likufotokozera:

Chibvumbulutso 22:1 Ndipo anandionetsa mtsinje wa madzi a moyo, wonyezimira ngati Krustalo, otuluka kumpando wacifumu wa Mulungu ndi wa Mwana wankhosa.

Yohane 15:26 Koma pamene wafika Nkhoswe, amene Ine ndidzamtuma kwa inu kuchokera kwa Atate, ndiye Mzimu wa coonadi, amene aturuka kwa Atate, Iyeyu adzandicitira Ine umboni.

Aroma 8:9,10 Koma inu simuli m'thupi ai, koma munzimu, ngatitu mzimu wa Mulungu akhalabe mwa inu. Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, siali wace wa Kristu. Ndipo ngati Kristu akhala mwa inu, thupilo ndithu liri lakufa cifukwa ca ucimo; koma mzimu uli wamoyo cifukwa ca chilungamo.

Ichi ndi chifukwa Yesu atchedwa kuti ndi nzeru ndi mphamvu ya Mulungu. Chikhalidwe cha Yesu chitumizidwa kudzala m’Mzimu wa Mulungu kuphyola mu chirengedwe kufikira cholengedwe chonse. Ndi nzeru ya Kristu yomwe imabwera m’mitima yathu yomwe imaphunzitsa ife momwe tingakondere ndi kumvera Mulungu; ndi moyo wa Kristu omwe umachititsa musepha uli wonse ndi minyewa yathu kuti tikhale ndi moyo.

1 Akorinto 1:24 Koma kwa iwo oitanidwa, ndiwo Ayuda ndi Ahelene, Kristu mphamvu ya Mulungu, ndi nzeru ya Mulungu.

1 Akorinto 1:30 Koma kwa Iye muli inu mwa Kristu Yesu, amene anayesedwa kwa ife nzeru ya kwa Mulungu, ndi cilungamo ndi ciyeretso ndi ciombolo;

Choncho ndi Mzimu wa Kristu mu munthu umene umawapatsa nzeru kuchita zolungama ndi za bwino. Solomoni adalakhulapo za izi ndi momwe nzeru ichtira mu chirengedwe:

Miyambo 8:12-21 Ine Nzeru ndikhala m’kucenjera, ngati m’nyumba yanga; ndimapeza kudziwa ndi zolingalira. Kuopa Yehova, ndiko kuda zoipa; Kunyada, ndi kudzikudza, ndi njira poipa, ndi m’kamwa mokhota, ndizida. Ndine mwini uphungu ndi kudziwitsa; ndine luntha; ndiri ndi mphamvu. Mwa ine mafumu alamulira; Akazembe naweruzza molungama. Mwa ine akalonga ayan’ganira, Ndi akuru, ngakhale oweruzza onse a m’dziko, Akundikonda ndiwakonda; Akundifunafuna adzandipeza. Katundu ndi ulemu ziri ndi ine, Cuma cosatha ndi cilungamo. Cipatso canga ciposa golide, ngakhale golide woyengeka; phindu langa liposa siliva wosankhika. Ndimayenda m’njira ya cilungamo, Pakati pa mayendedwe a ciweruzo, Kuti ndionetse cuma akundikonda, cikhale colowa cao, Ndi kudzaza mosungira mwao.

Ndipo adapitirira kufotokozero momwe Mulungu adabweretsera ndi kukhadzikitsa Mwana wake.

Miyambo 8:22-31 Mulungu anali nane poyamba njira yace, Asanalenge zake zakale. Anandiimika cikhaliye ciyambire, Dziko lisanalengedwe. Pamene panalibe zozama ndinabadwa ine, Pamene panalibe akasupe odzala madzi. Mapiri asanakhazikike, Zitunda zisanapangidwe, ndinabadwa; Asanalenge dziko, ndi thengo, Ngakhale ciyambi ca pfumbi la dziko. Pamene anakhazika mlengalenga ndinali pompo; Pamene analemba pazozama kwete kwete; Polimbitsa Iye thambo la kumwamba, Pokula akaakasupe a zozama. Poikira nyanja

malire ace, Kuti madzi asapitirire pa lamulo lace; Polemba maziko a dziko. Ndinali pambali pace ngati mmisiri; Ndinamsekeretsa tsiku ndi tsiku, Ndi kukondwera pamaso pake nthawi zonse; Ndi kukondwera ndi dziko lace lokhalamo anthu, Ndi kusekerera ndi ana a anthu.

Thokozani Atate chifukwa cha Mwana, popanda Iye chirengedwe sichikanagwira ntchito, palibe chiri chonse chikanagwira bwino. Tsopano tikuwona kukwanira kwa uwiri wa Umulungu wawo ukubwera pamodzi. Atate ndi Mulungu yekha wowona ndiye chiyambi ndi magwero a zonse. Anabweretsa Mwana wake kwa yemwe adapereka zonse. Kuzera mwa Mwana kumayendera china chiri chonse chofunikira kugwiritsira ntchito mu chirengedwe. Mwa Mwana mphamvu ndi nzeru kuphatikizana ndi kukhulupirira ndi kugonjera momvera. Chikhalidwe chake cha Mwana chimazera ku chirengedwe kupyolera mu Mzimu wa Mulungu wopezeka pali ponse. Iri ndi ndongosolo la nzeru kwambiri ndipo Mulungu ndi wanzeru kopambana kupanga ichi.

Paulo akufotokoza za ichi mwachidule modabwitsa pamene akuti:

1 Akorinto 8:6 Koma kwa ife kuli Mulungu mmodzi, Atate amene zinthu zonse zichokera kwa Iye, ndi ife kufikira kwa Iye; ndi Ambuye mmodzi Yesu Khristu, amene zinthu zonse ziri mwa Iye, ndi ife mwa Iye.

4. Chifanano

Mu mutu wambuyomu, tinawerenga za nzeru zodzidziswa za Mulungu pokhadzimitsa maziko a chirengedwe. Kubweretsa kwa Mwana kupasidwa zikhumbo zonse za umulungu anapereka kukwanira kwa Mulungu kutumizidwa m'mitima ya zorengedwa zonse kudzera m'Mzimu wa Mulungu. Chotsatira china chimene Mulungu anapanga ndi kupereka kufotokozerwa kwa makhalidwe okhalapo ofanana kusawerengera udindo mu chirengedwe.

Atate adapereka ulamuliro kwa Mwana wake kuti afanane ndi Iye. Dziwani momvetsetsa kuti kufanana ndi Mwana wake sikunabwera kudzera ku mphwamvu zomwe Mulungu adapereka kwa Iye, koma kupyolera mu ulamuliro ndi m'dalitso wa Atate. Ngati Mwana akadaganirizidwa kufanana ndi Atate ake chifukwa chakukhala ndi mphwamvu Yake, ndiye mafotokozeredwe a chifanano chimachokera mu mphamvu. Kafotokozeredweka kakanamuyika Mwana mu udindo osimikizira muchifanano chake zochokera mphamvu yake. Umu ndi momwe Satana adawumiriza Yesu muchipululu; chiwonetsero cha mphamvu kuti chisimikizire ubale wake ndi Atate ake. Zikomo kwambiri, Mwana amakhazikika m'dalitso la mau Atate. Mwana akhulupirira Atate ake, ndipo palibe chomwe angasimikizire kwa wina. Ubale wa Atate ndi Mwana unakhala liwulo la ubale wa chirengedwe. Ma ubale onse amadongosolo okhalamo akanatero potsatira pa ubale wawo. Atate anamupanga Mwana wake ofanana ndi Iye.

Afilipi 2:5,6 Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu. Ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu.

Yohane 5:22, 23 Pakuti Atate saweruzwa munthu ali yese, koma anapereka kuweruzwa konse kwa Mwana, kuti onse akalemekeze Mwana, monga alemekeza Atate. Wosalemekeza Mwana salemekeza Atate amene anamtuma Iye.

Njira ya nzeruyi anaonetsera kuti tanthauzo la kufana kukanatero mu kuchuluka kwa ubale. Pachifukwa ichi tikuthandawudza kuti ubale ofotokozeredwa ndi Atate omwe achititsa kufanana. Mphamvu zonse Mwana alinazo, nzochokera kwa Atate ake ndipo sizimakhadzimitsa mbali ya kufotokozerwa kwa chifanano. Zimakhala zopanda phindu mumachitidwe ofanana. Mulungu adachita izi ndi cholinga choti olengedwa asamadzifanize

okha pa lunso ndi kuthekera, komwe adalandira, koma kuti kudzera kwa kuthekera kwao mukudziwa ndi kumvetsetsana wina ndi mzake.

Chikhalidwe cha chifanano cha Atate kwa Mwana ndi chofunikira kwambiri pa kufotokozera ku chirengedwe chonse. Ngati sitimvetsetsa bwino za ubalewu ndiye kuti sitimvetsetsa bwino kwenikweni za ufumu wa Mulungu. Chimodzi mwa zinthu zodabwitsa cha Mwana wa Mulungu ndichoti amadziwa chirichonse chimene chiripo chodziwa za Atate. Palibe ofanana ndi Iye yemwe angafotokozere ku chirengedwe chonse mmene Mulungu aliri. Onani momwe Yesu akufotokozera za kufana kwa Iye ndi Atate mumau a ubale:

Yohane 10:15 monga Atate andidziwa Ine, ndi Ine ndimidziwa Atate; ndipo nditaya moyo wanga chifukwa cha nkhosha.

Choncho Yesu akutha kunena motsimikiza:

Yohane 14:9 iye amene wandiona Ine waona Atate;

Mauwa si achinsinsi a thunthu limodzi; ndi mau amene Yesu akudziwa za Atate ake ndikuti anadzazidwa ndi khalidwe ndi maonekedwe ake. Palibe wina mu chirengedwe chonse amadziwa maganizi a Atate kufanana ndi mmene Iye amadziwira maganizo a wina ali yense - ndi Mwana yekhayo basi. Ubale wawo umawonetsera amene timapembeza ndi ubale wachikondi pakati pawo kusiyana ndi mphamvu yimene ali nayo limodzi.

Mneneri Yeremiya akuwulula za ulemerero wa ufumu wa Mulungu pamene Iye akunena:

Yeremiya 9:23, 24 Atero Yehova, wanzeru asadzitamandire m'nzeru zace, wamphamvu asadzitamandire m'mphamvu yace, wacuma asadzitamandire m'chuma cace; koma wakudzitamandira adzitamandire adzikweze umo, kuti ali wa kuzindikira, ndi kundidziwa Ine, kuti ndine Yehova wakucita zokoma mtima, ciweruziro, ndi cilungamo m'dziko lapansi, pakati m'menemo ndikondwera, ati. Yehova.

Choncho tapeza kufotokozedwa kwa chifanano chomwe chikhazikisa kamvekedwe konse ka Ufumu wa Mulungu womangidwa kwambiri pa mayina a Atate ndi Mwana ndi mmene amakhudzirana wina ndi nzake. Kugawana kwa mphamvu kwa Mwana ndi Atate sikusimikizira ndi china

chake chomwe Iye yekha angabweretse mu mphamvu ndi udindo, koma pa chifuniro ndi chisangalalo cha Atate okha.

Afilipi 2:9 Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa Iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse.

Ahebri 1:6 Ndipo pamene atenganso wobadwa woyamba kulowa naye m'dziko, anena, ndipo amgwadire Iye angelo onse a Mulungu.

Luka 9:35 Ndipo munatuluka mau mumtambo nanena, Uyu ndiye Mwana wanga, wosankhidwayo; mverani Iye.

Kufanana kwatsamira pa ulamuliro wa Atate, osati pa zikhumbo za Mwana wake. Mukufotokozeraku kwa Atate ndi Mwana mukumapitiriza mayina awo payekha payekha, koma ali ofanana.

Chotsatira cha njirayi sichingawoneke poyamba, koma zotastira pa banja la munthu ndi zazikulu, makamaka pamene tinena za kufanana pakati pa adzibambo ndi adzimai ndimene zimawafokozera iwo.

5. Chifuniro

Tsopano tikutha kuwona kuti Mzimu wa Mwana wa Mulungu umatsefukira ku chirengedwe chonse chokhalamo ndipo amakhala m'mitima ndi m'malingalilro awo onse. Kuti chirengedwe cha Mulungu chikhaledi cha ubale mowonadi, zolengedwa zonse zinayenera kukhala ndi kuthekera kosankha kuvomera kapena kukana Mzimu wopereka Moyoyu wa Mwana. Kopanda mphamvuyi yakusakha, chirengedwe chonse chikanakhala kwambiri chongozichitira pachokha ngati makina opangiridwa zoti achite (robotic). Mulungu wapereka ku chirengedwe chonse cha makhalidwe a chifuniro ndi mphamvu yosankha. Mphamvuyi yosankha yiri ndi malire amodzi okha a chisankho: kumukonda Mulungu ndi kumuvomera Iye ndi moyo Wake wopereka Mzimu kupyolera mwa Mwana Wake kapena kukana moyo Wake ndi kubweresa ifa pa ife eni.

Yoswa 24:15 Ndipo ngati kutumikira Yehova kukuipirani mudzisankhire lero amene mudzamtumikira, kapena milungu imene anaitumikira makolo anu okhala tsidya lija la mtsinje, kapena milungu ya Aamori amene mukhala m'dziko lao; koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova.

Miyambo 3:5, 6 Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, osacirikizika pa luntha lako, Umlemekeze m'njira zako zonse, ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako.

Mphamvu yakusakha itanthawuza kuti wina ali yense azitengera umwini wa moyo wamakhalidwe a Mwana wa Mulungu. Chikondi cha Mwana kwa Atate chimakhala chikondi chathu; kugonjera ndi kudalira kwa Mwana wa Mulungu zimakhala kugonjera ndi kudalira kwathu. Chilungamo chake chimakhala chathu pamene tipitiriza chisankho chogonjera. Kuthekera kwa kugonjera ndi kusankha pachiyambi zimabwera mwaufulu kupyola m'mtsinje, koma monga tiwonere, vuto linabwera ku chirengedwe limene linasokoneza banja la Mulungu ndi kubweretsa madzunzo kwa onse.

6.Vuto liyamba

Ndi zonse m'malo, Mwana wa Mulungu anapasidwa ntchito yolenga chirengedwe. Kupyolera Mphamvu ya Atate ake, Iye analenga nyenyezi zonse, mayiko ndi zamoyo zonse. Iye analenga khamu la angelo, woyamba mwa iwo anamutcha Lusifala - wonyamula kuwala.

Yohane 1:1-3 Pachiyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu. Awa anali pachiyambi kwa Mulungu, Zonse: zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa.

Aefeso 3:9 ndi kuwalitsira onse adziwe makonzedwe a cinsinsico, cimene cinabisika ku yambira kale kale mwa Mulungu wolenga zonse;

Aheberi 1:1, 2 Kale Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyana-siyana, koma pakutha pace pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe;

Lusifala anadziwa udindo wa Mwana wa Mulungu ndikuti analandira Umulungu wonse ngati cholowa. Iye anayamba kutaya masomphenya a nzeru ya Mulungu mwa Mwana Wake. Kupyolera mu mphatso ya chifuniro, iye anayamba kufunsa pa chifukwa chanji Mwana wa Mulungu angakhale ofanana ndi Mulungu. Iye anayamba kusirira udindo wa Mwana, ndipo anaganizira kuti ngati Mwana angalandire udindowu nanga iye osalandira bwanji? Chifukwa chiyani osakhala wina wachitatu ngati Mulungu? Iye sanamvetsetse kufunikira kwa udindo wa Mwana ndi Mzimu wake wogonjera amene anachirikiza chirengedwe chonse pamodzi.

Akolose 2:9,10 pakuti mwa Iye chikhalira chidzalo cha Umulungu m'thupi, ndipo muli odzazidwa mwa Iye, ndiye mutu wa ukulu wonse ndi ulamuliro;

M'malo mosamalira chizindikiro ndi khalidwe la Mulungu ndi Mwana Wake, iye anayamba kusirira mphamvu ndi udindo wa Mulungu. Limodzi mwa malingalira ake kunali kuti ngati Mwana anabadwa kuchokera kwa Mulungu ndiye kuti Iye sangafanane Naye. Iye anadabwa chifukwa chiyani iye apembeze wina amene sali ndi mphamvu payekha ndikuti amadalira wina kuti akhaleko. Anafika pa ganizo loti iye aloledwe kukhala pa udindo ofanana

ndi Mwana kapena kuti iye aganize kuti sanakonderedwe ngati Mwana kufanana ndi Mulungu.

Aefeso 2:5,6 tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Kristu {muli opulumusidwa ndi cisomo}, ndipo anatiukitsa pamodzi, natikhadzikitsa pamodzi m'zakumwamba mwa Khristu Yesu;

Yesaya 14:12-14 Wagwadi kucokera kumwamba, iwe nthanda, mwana wa mbanda kuca! Wagwetsedwa pansu, iwe wolefula amitundu! Ndipo iwe unati mumtima mwako, Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wacifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu, m'malekezero a kumpoto; ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi Wam'mwambamwamba.

Ezekiele 28:14,15 Unali kerubi wodzozedwa wakuphimba, ndipo ndinakuika unali pa phiri lopatulika la Mulungu, anayendayenda pakati pa miyala yamoto. Unali wangwiro m'njira zako cilengedwere iwe, mpaka cinapezeka mwa iwe cosalungama.

Lusifala anati m'mtima mwake kuti iye azakhazikisa mpando wake wachifumu pamwamba pa nyenyezi kapena kuti angelo a Mulungu. Iye akwera kufika pa udindo wa Wam'mwamba-mwamba. Lingaliro lake lonse linali loti apeze mphamvu ndi udindo. Panalibe khumbo la khalidwe la Mulungu, koma kokha udindo Wake ndi mphamvu.

Ndi chinsinsi momwe Lusifala anayamba kuganiza mu njirayi. Baibulo siritiiza ife, koma chifukwa Mulungu anapereka ku zolengedwa zake mphamvu yosakha, Lusifala anagwiritsa mphamvuyi kutembenuka mtima wake kuchoka ku nzeru ya Mulungu ndi kugonjera kwa Iye ndi dongosolo Lake la chirengedwe.

Mulungu anayesa kuweruzana ndi Lusifala njira imene anatenga. Anafotokozeredwa Iye zifukwa zomwe Mwana wa Mulungu anakhalira ndi uindowu. Koma Lusifala anakana kumvera ndikukhala Satana - oneneza. Iye ananeneza Mulungu kuti wakhazikitsa ufumu wolakwika ndikukana kupembeza Mwana wa Mulungu. Iye anasankha ndi kusimikizika m'malo mwake ngati safanana ndi Mulungu ndiye kuti avomera kokha Mulungu amene analandira mphamvu mwa Iye yekha osati kwa kulandira kwa wina wake.

Apa pali nfundo yofunikira kwambiri yofuna kunena. Mulungu yekha ndiye magwero a moyo. Kusagwiriza ndi Mulungu ndi kukana kudalira ndi kumvera lye pomwepo umazichosa ku moyo. Moyo umachokera kokha pa kugonjera kwa Mulungu ndipo kugonjera kokha kumabwera kwa ife kuzera mwa Mzimu wa Mwana. Iyi ndi nfundo yafunikira kwambiri mwa zina chifukwa Atate ndi Mwana awiriwa are ofunikira kwambiri. Pa kukana kugonjera, Lusifala amakana Mzimu wa Mwana waku gonjera. Ntchito yokana ndi ntchito ya madano ndi kupha. Ndichifukwa chake maganizo a thupi ndi odana ndi Mulungu.

Aroma 8:7 Cifukwa cisamaliro ca thupi cidana ndi Mulungu; pakuti sicigonja ku cilamulo ca Mulungu, pakuti sicikhoza kutero.

Pamene Satana anakana Mulungu, Mulungu mwachangu anayenera kupanga chisankho - chisankho lye anakonza, anayenera tsopano kukwanirisa. Pakukana Mulungu, Lusifala amati Ayi kwa Mzimu wa Khristu, amapha Mwana wa Mulungu. Iye amati ndikufuna mphamvu yanu, osati Mwana wanu. Mwina Mulungu akanamusiya Lusifala kuti pomwepo afe chifukwa chosiya gwero la moyo, kapena kulola Mwana Wake kuti afe monga m'mene Lusifala amalingalira m'maganizo ake. Ifa ya Kristu si ntchito ya chigamulo chachilungamo ku mbari ya Mulungu kuchita kubwezera; ndikuonetsera lamulo la chirengedwe za chirengedwe kuti moyo umochoka kwa Mulungu kokha ndi Mwana Wake. Lusifala sangapeze phindu kuchokera ku imfayi chifukwa iye anakana kusakha kuvomereza chizindikiro cha Mwana wa Mulungu; koma imfa ya Kristu ndi chuma chimene chikugwiridwa ntchito kumenyana ndi Satana ndi angelo ake kuti zolengedwe zonse zione zimene ziri m'maganizo a Satana. Ngati Lusifala akanafa m'malo mwa Mwana kutenga ganizo limeneli pachiyambi, palibe amene akanamvetsetsa chifukwa ndipo Mulungu akanawopedwa m'malo mokondewda. Mwana wa Mulungu anapezeka pakati pa vuto la Satana lokana chifuniro cha Mulungu. Mwina Mulungu akanalola Satana afe kapena kulola Mwana wake afe, ndi chiyembekezo choti ife tize ndi kudziwa m'mene lye aliri. Umu ndim'mene imfa ya pa mtanda yiriri - kudziwa chizindikiro Chake chenicheni mu ufumu wa Mulungu.

Yohane 17:3 Koma moyo wosatha ndi uwu kuti akadziwe Inu Mulungu woona yekha, ndi Yesu Kristu amene munamtuma.

Satana anayamba kufalitsa malingaliro ake kwa ena kotero kuti gawo lilodzi la atatu anaganiza kuti Lusifala akunena zoonza. Chifukwa chiyani ayenera kugongera kwa Mwana amene anapasidwa chiri chonse kuchokera kwa

Atate, ndichani chimene anali nacho chapadera-dera. Anakana kugonjera ku chifuniro cha Mulungu. Mwachisoni nkondo ya mau inabuka ku mwamba ndipo Satana ndi omutsatira ake anachotsedwa kumwamba.

Chivumbulutso 12:7-9 Ndipo kunali nkondo m'mwamba. Mikayeli ndi angelo ace akucita nkondo ndi cinjoka; cinjokanso ndi angelo ace cinacita nkondo; ndipo sicalakika, ndipo sanapezekanso malo ao m'mwamba. Ndipo cinaponyedwa pansu cinjoka cacikulu, njoka yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansu kudziko, ndi angelo ake anaponyedwa naye pamodzi.

Mulungu akadalola Satana kufa, koma mbeu ya malingaliro ake owopsya adayenera kuloredwa kuti akhwine ndipo awonekere. Monga Satana adakana moyo wokhawo wopezeka kwa iye kupyolera mwa Mwana wa Mulungu, iye akanalodwa kuti awonongeke, koma angelo ndi chirengedwe chonse chikana yamba kulingalira kuti Mulungu anangomuwononga iye mwankhaza chimene chikanatsogolera ku ganizo loti Mulungu ndi wachiwawa mwa chikhalidwe. Aliyetse akadayamba kuphunzira payekhapayekha chifukwa chomwe moyo ndiwothekera ku chirengedwe kudzera mwa Mwana . Aliyense muchirengedwe ali ndi mwayi wosankha yemwe ali wolungama; Mulungu kapena Satana.

7. Kulengedwa muchifanizo chake

Satana ndi gawo limodzi la atatu a angelo adafunsa za udindo wa Mwana ndi ubale Wake ndi Atate Ake. Panalibe amene akanatsimikizira chiyambi cha ubale wa Atate ndi Mwana ndipo chomwecho akadayenera kudalira Atate kuti Iye ndi amene amadziwa chabwino cha wina aliyense.

Podziwa kuti idzafika nthawi yoti ubale wa Atate ndi Mwana Wake udzafunsidwa, Mulungu anakhazirathu dongosolo lofotokoza mwakuya la ubale wapadera - dera umene Iye anawuchirikiza ndi Mwana Wake. Iye anayerera kupereka chisanzo ku chirengedwe kuti awone mwakuya kwambiri mphamvu ya umutu ndi chigonjero mu ubale wa Atate - Mwana.

Panali pamene Atate ndi Mwana anali pa dongosolo lopanga dziko la pansi kukhumudwa kwa Lusifala kunachuluka. Lusifala anakhumba kukhala Kalonga wa dzikoli koma pempho lake linakanidwa. Kristu ndi amene akhala Kalonga wa dzikoli chifukwa dzikoli lipangidwa mu chifanizo cha Atate ndi Mwana Wake. Lusifala anakhala ndi nsanje ndi Mwana wa Mulungu. Ngati Lusifala akanadalira kuti dongosololi likanamuthandiza kumvetisa ubale wapadera-dera pakati pa Atate ndi Mwana ndi chifukwa choti ntchito ya Mwana yinali yofunikira kwambiri ku ufumu wa Mulungu. Mwachisoni, sizinayenera kukhala choncho.

Mulungu ndi Mwana Wake anapitiriza dongosolo lolenga dziko la pansi ndi kuulula ku chirrengedwe chifanizo chapadera-dera cha ubale wawo. Ndipo Mulungu anati kwa Mwana Wake, "Tipange munthu m'chifanizo chathu." Gen 1:26.

Ndani angamvetsetse za ntchito yayikulu kwambiri ya kulenga mu sabata la (mlungu wa) kulenga ! Tsiku ndi tsiku, pamene mphamvu ya kulenga ya Mulungu imasefukira kuchokera mwa Mwana Wake, dziko linatenga mawonekedwe. Nthaka, udzu ndi maluwa, mitengo, dzuwa ndi mwezi, zinyama, ndipo zonse zinakonzedwa za chimake cha chirengedwe - kulengedwa kwa munthu mwamuna ndi mkazi.

Ntchito ya kulenga ndiyofunikira kwambiri ndipo imanena za nkhani yofunkira yokhuzana Mulungu nd Mwana Wake.

Genesis 1:27 Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifaniziro cake, m'cifanizo ca Mulungu adalenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi.

Umu ndi momwe ntchitoyi idakhalira:

Genesis 2:7 Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira mphweya wa moyo m'mphuno mwace; munthuyo nakhala wamoyo.

Genesis 2:18-25 Yehova Mulungu ndipo anati, sikwabwino kuti munthu akhale yekha ; ndidzampangira womthangatira iye. Ndipo Yehova Mulungu anaumba ndi nthaka zamoyo zonse za m'thengo, ndi mbalame zonse za m'lengalenga; ndipo anapita nazo kwa Adamu kuti aone maina omwe adzazicha; ndipo maina omwe onse anazicha Adamu za moyo zonse, omwewo ndiwo maina ao. Adamu ndipo anazitcha maina zinyama zonse, ndi mbalame za m'mlengalenga ndi za moyo zonse za m'thengo: koma kwa Adamu sanapezedwa womthangatira iye. Koma Yehova Mulungu anamgonetsa Adamu tulo tatikulu, ndipo anagona; ndipo anatengako nthiti yace imodzi, natsekapo ndi mnofu pamalo pake. Ndipo nthitiyo anaichotsa Yehova Mulungu mwa Adamu anaipanga mkazi, ndipo ananka naye kwa Adamu. Ndipo anati Adamu, Uyu tsopano ndiye fupa la mafupa anga, ndi mnofu wa mnofu wanga; ndipo adzatchedwa mkazi, cifukwa anamtenga mwa mwamuna. Cifukwa cotero mwamuna adzasiya atate wace ndi amace nadzadziphatika kwa mkazi wace: ndipo adzakhala thupi lomdzi. Onse awiri ndipo anali amarisece, mwamuna ndi mkazi wace, ndipo analibe manyazi.

Mulungu, kudzera kwa Mwana wake, adawumba Adamu kuchokera kufumbi la dziko, kenako mtsinje wa moyo unatsefukira kapena kuti unauwudziridwa mwa iye. Makhalidwe a mtengo wapatali a Mwana wa Mulungu, m'lingaliro wa m'dalitso wa Atate ndi kudalira kwa chikondi ndi kumvera kwa Mwana, mokondwa anadutsa mu chifuniro cha Adamu ndikukhala gawo lake. Adamu mwachibadwa amakhumba kutumikira Mulungu ndi kumukondweretsa Iye, chifukwa iye amalandira makhumbowa kuchokera kwa Mwana wa Mulungu kupyolera mu Mzimu.

1 Akorinto 2:16 Pakuti wadziwa ndani mtima wa Ambuye, kuti akamlangize Iye? koma ife tiri nao mtima wa Kristu.

Mulungu adakhadzikitsa Adamu munyengo yoti ayambe kuphunzira kuti chinachake chinali kusowa. Ndi chifukwa ninji Mulungu adapanga Adamu yekha kumudutsitsa munyengo yosowa chinachake? Ichi chikutiphunzitsa ife china chake chosangalatsa za Mulungu ndi ufumu Wake: Zithu zina tikhoza kuziphunzira kudzera mu zomwe zinachitika, ndipo kwa Adamu podzindikira

kuti china chake chikusowa chinakulisa khumbo lake ndi kukweresa m'lingaliro wothokoza pamene Mulungu anapereka chosowacho.

Adamu adasowa okhala naye yemwe akadamvetsa malingaliro ndi kuganiza kwake. Wina wake yemwe akayamikira chimwemwe chake ndikumvetsetsa za zomwe iyeyo wadutsamo. Pamene Adamu adatchula maina a nyama adayamba kudzindikira kuti palibe ofanana naye, palibe okumva za iye. Ichi chidakhadzikika mwa Adamu chikhumbokhumbo chomwe chinali gwero la ufumu wa Mulungu: ubale weni - weni. Ubaleu umapangisa m'lingaliro woti njira yokhayo yomvetsetsa ndi kudusamo muzochitika. Mulungu akanatha kumuusa Adamu za kufunikira kwa ubale ndi kumufotokozera ubwinowo, koma pomupasa ntchito Adamu popereka maina a nyama, zinamvetsetseka otsati mumalingaliro a Adamu okha ayi komaso mu mtima mwake, chomwe chinali chofunika.

Ndichifukwa chiyani Mulungu adamuchititsa Adamu kugona ndi kumung'amba thupi lake ndikutengako nthiti imodzi ndikupanga mkazi? Kodi izi sizikuwoneka ngati zosamvetsetseka pochita zithu? Njirayi ndiyolangiza kwambiri. Njira ya Eva kupangidwa kuchokera kwa Adamu, kupangidwa ndi thupi lake ndi kuchokera pa mbali yake pafupi ndi mtima wake, zikulankhula mwachindunji za nkhani ya Atate za momwe Mwana Wake anachokera kwa Iye. Kodi chifukwa ninji Mulungu sadatengapo mbali ya ubongo wa Adamu, kodi chifukwa ninji ntchitoyo idali nthiti pafupi ndi mtima? Baibulo sirinatifotokozere za izi, koma likufotokozera ine zakukonzanso za kumu ukulu omwe unali m'mtima wa Adamu wosoweka mnzake womumvetsetsa iye ndikumutumikira ngati womugonjera wake wosamalira mbewu yimene ananyamula.

Yohane 1:18 Kulibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse; mwana wobadwa yekha wakukhala pa cifuwa ca Atate, Iyeyu anafotokozera.

Yohane 8:42 Yesu anati kwa iwo, Mulungu akadakhala Atate wanu, mukadakonda Ine; pakuti ine ndinaturuka, ndi kucokera kwa Mulungu; pakuti sindinadza kwa Ine ndekha, koma Iyeyu anandituma Ine.

Miyambo 8:23-25 Anandiimika chikhalire chiyambire, Dziko lisanalengedwe. Pamene panalibe zozama ndinabadwa ine, pamene panalibe akasupe odzala madzi. Mapiri asanakhazikike, Zitunda zisanapangidwe, ndinabadwa.

Aroma 1:19-20 cifukwa codziwika ca Mulungu caonekera m'kati mwao; pakuti Mulungu anacionetsera kwa iwo. Pakuti cilengedwere

dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula;

Pamavesi angolembedwawa, tikuwona umboni wa Mwana wa Mulungu akuchokera mu chifuwa Chake. Mau woti anatuluka ndi anabwera amatanthauza kuti 'anatuluka kuchokeramu' ndipo Miyambo 8:25 (Mapiri asanakhazikike, Zitunda zisanapangidwe, ndinabadwa); akufotokoza mwachindunji za kubadwaku. Mtumiki Paulo akuthirirapo ndemanga pakuyankhulaku kuti chirengedwe chikutipasa ife chithunzi mwachindunji za Uwiri mu Umulungu kuti tisowe chowiringula.

Ndani angalingalire zimene Adamu amaganizira pamene anawona Eva koyamba, pamene maso awo anakumana ndi kuzindikira kunabwera kuti pano pali wina amene angathe kumumvetsetsadi ndi kumuyamikiradi iye. Wina amene ali wa thupi lake ndiponso wina amene anganyamule mbewu yake, kuyisamalira ndi kukhala womugonjera. Mulungu anakhazikisa ufumu wa dziko lapansi kuti mwamuna asapange ufumu popanda mkazi wake. Ana ake sakanatha kudziwa makhaliidwe wogonjera popanda chisanzo cha moyo mwa mayi awo.

Pali chinthu chopatulika kwambiri chiripo pakati pa mwamuna ndi mkazi wake. Ubaleu ukapangidwa bwino umayankhula mwachindunji za ubale wa Atate ndi Mwana ndi chikumbutso chokhazikika ku chirengedwe za bodza la milandu ya Satana motsutsana ndi Mwana wa Mulungu.

1 Akorinto 11:10 koma mkazi cifukwa ca mwamuna; cifukwa ca ici mkazi ayenera kukhala nao ulamuliro pamutu pace, cifukwa ca angelo.

Mulungu adakonza ubale wa mwamuna ndi mkazi kukhala langizo kwa angelo za ubale wa Atate ndi Mwana. Mwayi wodabwitsa wotani nanga kulengedwa ndi cholinga chotere.

Kudziwa choonadichi, tikhoza kupeza chinsinsi cheni - cheni cha ukwati ndikulolera ife tokha kukokedwa ndi Mzimu wa Mulungu mu fanizo la ubale wa Atate ndi Mwana; mwamuna kukhala ngati gwero la dalitso ndi mkazi kukhala ngati chiwonetsero cha moyo wa chikondi chodalira ndi kugonjera.

Adamu ndi Eva adapasidwa maitanidwe apamwamba ndi wokondwa. Koma ngati iwo akanakhala mu chifanizo cha Atate ndi Mwana, ndipo mavuto wochulukira akanapewedwa.

8. Tate wa Mabodza

Tikukumbukira kuti Satana adachita chisankho kuti ngati samulola iye kupeza mphamvu ndi maudindo a Mwana wa Mulungu akadachita chisankho chomupembedza Mulungu yekha wokhala ndi mphamvu za mwa Iye yekha zimene zinali zosapasidwa. Pamene Mulungu adakana kubvomeredza maganidzo a Satana '**okonza**', Satana anayikidwa pa mulingo wovomereza kuti iyebe ali ndi ngongole ya moyo kwa Mulungu, ngakhale sangavomeredze udindo waukulu wa Mwana.

Panalibe njira Satana akanatha kukhadzikitsa ufumu wake kukhazikika pa mfundo zake zokha ngati nthawi zonse amazindikira kuti mphamvu zonse zimachokera kwa Mulungu. Choncho anapeka bodza lalikulu - loti Aliyense ali ndi moyo mwa iye yekha. Panali njira zingapo zokhulupirira njirayi. Ukhoza kukhulupirira kuti uli wosafa ndikuti kusafa ndi khalidwe mwachirengedwe la cholengedwa chonse. Ukhoza kukhulupirira kuti moyo umakhalapo ngati mphamvu basi ndi kuti aliyense ndiwolumikizika ku iyo ndipo ungayigwirise pochita chiri chonse iwo afuna. Kapena ukhoza kukhulupirira mwa Mulungu amene apereka mphatso ya moyo wosafa kuugwiritisa ntchito m'mene ungathere. Palibe kanthu usankha kukhulupirira njira yanji, chachikulu ukhulupirira uli ndi gwero lakolako la moyo mwa iwe wekha. Iri ndi bodza lalikulu kwambiri m'chirengedwe. Monga Yesu anati:

Yohane 8:44 Inu muli ocokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolakalaka zace za atate wanu mufuna kucita. Iyeyu anali wambanda kuyambira paciyanbi, ndipo sanaime m'coonadi, pakuti mwa iye mulibe coonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wace; pakuti ali wabodza, ndi atate wake wa bodza.

Mulungu akanatha kuthetsa bodzali pomwepo pochititsa kuti onse omwe anakana Mwana Wake amwalire, koma Mwanayo anapitirirabe kuwapasa moyo ngakhale zinali zomupweteka Iye. Ndicholinga choti chirengedwe chione zosatira za bodza, Mwana anayenera kuwanyamula angelo akugwawo ndikuwapasabe iwo moyo ngakhale iwo amakhumbabe kupha ndi kuwononga Iye. Pamene Satana ndi angelo ake anamukana Yesu, sadalandirensa Mzimu wogonjera ndi kumvera kuchokera kwa Iye. Ndipo anapachika kwa iwo okha Mwana wa Mulungu mu khalidwe Lake ndi Mzimu ngakhale Mulungu adapitiriza kuwapatsa iwo mphamvu ya moyo kuti Satana akhale ndi nthawi kuwonetsera nzeru zake. Mulungu adachita izi kulola chirengedwe chisankhe amene akudziwa njira yabwino kwambiri. Monga tamwa poyamba, panali mtengo polola Satana kukana Mulungu - mtengo ndi

moyo wa amene amakanidwa ndiye Mwana wa Mulungu. Satana adali wakupha kuchokera pa chiyambi; anachititsa ifa ya Kristu pamene iye amamukana Mulungu. Ifayi imachitika m'malingaliro a Satana, ndipo izi zimafuna kuti ziwonetsedwe ku chirengedwe kuti aliyense awone chimene chimachitika. Sichinali cholinga cha Mulungu kuti chiwonetserochi chichitike pa dziko la pansu, koma zachisoni ndimumene zinachitikira.

9. Kukopeka kwa anthu

Mugawo lapitalo tinawona kufunikira kwa chifuniro. Mphatso ya chifuniro chopasidwa kwa amuna ndi amai zimaalola iwo kusankha kugonjera kwa Mulungu. Popanda kuthekera kosankha kugonjera palibe m'dalitso weniweni kapena m'lingaliro lokondweretsa Atate. Ndi m'lingaliro lokondweretsa Atate limene limabweretsa m'dalitso. Onani m'mene Yesu akunenera:

Yohane 8:29 Ndipo wondituma Ine ali ndi Ine; sanandisiye Iye pa ndekha; chifukwa ndichita Ine zimene zimkondweretsa Iye nthawi zonse.

Yesu adali ndi m'lingaliro lokhazikika la m'dalitso kupyolera ku gonjero lopitirira la chifuniro Chake ku chifuniro cha Atate. Mphatso ya chifuniro imamabala madalitso ena ochuluka kuposa apa, koma nzosamvetsetseka pa nthawiyi. Pamene Mulungu adalenga Adamu ndi Eva, Mulungu adawapatsa mwai otha kuchita chifuniro chawo. Opanda kuthekera kukondweretsa Mulungu, palibe kuthekera kulandira m'dalitso wokondweretsa Iye.

Mulungu anakhadzikitsa mphamvu yokondweretsa Iye pomupasa mwayi omukana Iye pakudya za Mtengo Wodziwitsa Chabwino ndi Choyipa.

Genesis 2:16,17 Ndipo Yehova Mulungu anamuuzza munthuyo, nati, mitengo yonse ya m'munda udyeko; koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa usadye umenewo; chifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu.

Pamene amasankha tsiku ndi tsiku kutsadya kuchokera ku mtengo wapaderawu, Adamu ndi Eva adalandira m'dalitso wa padera wogonjera; m'lingaliro loti Mulungu amakondwera nawo. Popanda mtengowo kukhala pamenepo, sakadalandira m'dalitsowo.

Ngakhale Satana adamuchotsa kumwamba, adapatsidwa mwai ku dziko lathu lapansi kudzera malo amodzi komwe mwai wokusamukondweretsa Mulungu kukhoza kuchitika. Ichi ndi chifukwa tikupedza kuti Satana anali mu chifanizo cha njoka, kukhala m'Mtengo wa Kudziwitsa Chabwino ndi Choyipa. Tikudziwa kuti njokayi ndi Satana kuchokera mu buku la Chibvumbulutso:

Chivumbulutso 12: 9 Ndipo cinaponyedwa pansi cinjoka cacikuru, njoka yokalamambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko nse; cinaponyedwa pansi pa kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi.

Kuchokera pa zomwe taphunzira zokhudzana ndi Satana mafikidwe ake ku moyo, pofuna kumukopa Adam ndi Eva ku ufumu wake anakabweretsa maganizo kwa iwo momwe tingalandire moyo ochotsera kufuna kudalira pa Mulungu. Tamvani momwe Satana adanena:

Genesis 3:1-5 Ndipo njoka inali yakucenjera yoposa zamoyo zonse za m'thengo zimene anazipanga Yehova Mulungu. Ndipo inati kwa mkaziyo, Ea! kodi anaitu Mulungu, Usadye mitengo yonse ya m'mundamu? Mkazi ndipo anati kwa njoka, Zipatso za mitengo ya m'mundamu tidye. Koma zipatso za mtengo umene uli m'kazi mwa munda, Mulungu anati, Musadye umenewo, musakhudze umenewo, mungadzafe. Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, kufa simudzafai; cifikwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo, adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala ngati milungu, wakudziwa zabwino ndi zoipa.

Satana ankanthauza kuti potsakondweretsa Mulungu pokana zomwe lye analumulira sizingathe kubweretsa temberero koma m'dalitso; maso awo akanatsegulikira ku chidwitso chachikulu ndi nzeru ndipo iwo eni akanakhala ngati milungu. Iye anati kuti iwo safa, chimene chimathandauza kuti amawaphunzitsa kuti iwo akanatha kukhalabe ndi moyo popanda kudalira pa kapena kukhulupirira Mulungu. Iwo atha kuzidalira okha ndi chiwerudzo chawo eni.

Chisoni kuti Eva anavomeredza malangizo a chinjoka chija, ndipo adapitanso kwa Adamu pomunyengerera kutsakhulupira Mulungu koma kukhulupirira bodza lalikulula njokayo. Atangodya chipasocho ndikukhulupirira bodzalo, kuzindikira kwawo konse za Mulungu, za iwo eni, ndimene chirengedwe chikuyendera zinasinthirathu.

Povomeredza bodzali, Adamu ndi Eva anachoka pachikhulupiriro choti zinthu zonse zimachokera kwa Atate. Anakana ganizo loti chimwemwe chawo chinadalira pa chikhulupiro ndi kugonjera kwa Atate. Pokana ulumuliro wa Mulungu iwo anapha zedi makalidwe wokongola kwambiri a Mwana wa Mulungu - chikhulupiriro chomvera ndi kugonjera. Mulungu anayenera kuwonetsera Adam ndi Eva kuti kuleka kugonjera kwa Mulungu zinathandawudza kuwukira Mwana wake ndi zonse zimene lye anayimira. Adamu ndi Eva adapha mwana wa Mulungu m'mitima mwawo pokana mzimu wogonjera, omwe ndi Mzimu wa Mwana wa Mulungu. Iyi ndi mfundo yofunikira kwambiri kuyimvetsetsa. Chikhalidwe chokana Mulungu ndi chikhalidwe chakupha Mzimu wa Mwana, wogonjera kwenikweni.

Nchifukwa chake Yesu akutsimikidza kuti Lusifala ndi wakupha kuchokera pa chiyambi:

Yohane 8:44 Inu muli ocokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolakalaka zace za atate wanu mufuna kucita. Iyeyu anali wambanda kuyambira paciyambi, ndipo sanaime m’coonadi, pakuti mwa iye mulibe coonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wace; pakuti ali wabodza, ndi atate wace wa bodza.

Onse angelo omwe adamukana Mwana wa Mulungu ndikudana ndi Iye, adamupha Iye m’mitima mwawo. Baibulo likulumikiza momveka bwino udani ndi kupha:

1 Yohane 3:15 Yense wakudana ndi mbale wace ali wakupha munthu; ndipo mudziwa kuti wakupha munthu ali yense alibe moyo wosatha wakukhala mwa iye.

Nsembe ya Mwana wa Mulungu idawonekera pachiyambi dzikoli lisanalengedwe. Njira yokhayo yoti chirengedwe chimvetsetse zimene zinali m’mitima ya angelo wowukira yinali kuti ziwonekere poyera. Tamvani:

1 Petro 1:19, 20 koma ndi mwazi wa mtengo wake wapatali monga wa mwana wankhosa wopanda cirema, ndi wopanda banga, ndiwo mwazi wa Kristu: amene anazindikirikatu lisanakhazikike dziko lapansi, koma anaonetsedwa pa citsiriziro ca nthawi,

Mulungu sanadzidzimuke ndi kuwukira kwa Satana, Iye adakonzekera za izi; Mulungu ndi Mwana mu uphungu limodzi anakonza njira ya chipulumutso, koma kuwukira kwa Satana kunapangadi ndithu kufunikira kwa njirayi kuti ikwanitsidwe. Pomwe adafuwula kuti “ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndizafanana ndi Wam’mwambamwamba” panalibe mpata kwa Mwana wa Mulungu pa ganizoli; Iyeyo kunali kuchotsedwa ndi kuwonongedwa.

Satana anadzala mbewu yake yowukira mwa anthu ndipo Mwana tsopano anakayenera kuwafera iwo. Kristu anayenera kuwonetsera ku dziko kuti anthu apha Mwana wa Mulungu wogonjera m’mitima mwawo. Izi zinafunikira kudziwonetsera kwa wina ali yese. Pomupachika Mwana wa Mulungu pamtanda, tikuwona ntchito ya njoka kuwonekera. Iyi ndi mbali yina m’mene Mose analamulidwa kuyika njoka yamukuwa pa mtengo; ntchito yopachikidwa yinali yoyika poyera chiwembu chakupa cha Satana. Sakanathanso kubisa cholinga chake chenicheni kwa Kristu.

Pamene Adamu ndi Eva anachimwa ndikukana kugonjera Mzimu wa Kristu iwo anapezeka kuti ali ndi mlandu wakupha pamodzi ndi Satana. Kristu anaphedwa m'mitima ya Adamu ndi Eva.

Chivumbulutsa 13:8 Ndipo adzambilambira onse akukhala padziko, amene dzina lao silinalembedwe m'buku la moyo la Mwanawankhosa, wophedwa kuyambira makhazikidwe a dziko lapasi,

Aheberi 6: 6 koma anagwa m'cisokero; popeza adzipacikiranso okha Mwana wa Mulungu, namcititsa manyazi poyera.

M'chitidwe wakupha Mwana wa Mulungu chinaperekedwa ngati chidzindikiro kwa Adamu ndi Eva motere:

Genesis 3:21 Yehova Mulungu ndipo anapangira Adamu ndi mkazi wace maraya azikopa, nawaveka iwo.

Malaya achikopa anachokera ku zinyama. Nyamazi zinayenera kuperekedwa nsembe kuti Adamu ndi Eva abvekedwe. Adamu ndi Eva sadafune dzovala m'pakana atachimwa. Adabvekedwa ndi ulemelero wa Mulungu, koma atamukana Mulungu, anataya ulemelero. Kupha nkhosa chinali chindikiro cha lonjezano la Mulungu kutumiza Mwana Wake makamaka kuwawonetsera chimene anachita m'mitima yawo. Kuwathandiza iwo kuti awone chinthu chowopsyachi chokana Mulungu; ndi temberero lowopsya pamene takana kugonjera. Zimadula Mwana Mulungu - kugonjera kwenikweni.

Genesis 3:15 ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace.

Yohane 1:29 M'mawa mwace anaona Yesu alinkudza kwa iye, nanena, Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene acotsa cimo lace la dziko lapansi!

Chodzidziswa kwambiri Mwana wa Mulungu kuzichepetsa chonchi. Iye anayenera kuonetsa chirengedwe kukana kugonjera kumachita; kumapha munthu ofunikira kwambiri amene Mulungu amamukonda - Mwana Wake. Mwana wa Mulungu anayankha ku tsoka la kukana ndi chiwonetsero chosaneneka cha kugonjera; chiwonetsero cha mphamvu kwambiri chimene chirengedwe sichikhalaso chofanananso. Chiwonetsanso chirengedwe m'mene Mwana wa Mulungu ali wa mtengo wapatali kwambiri ndikuti timanyadira ndi kuyamikira Iye paku nyadira ndi kuyamikira Mzimu Wake wogonjera kwa Atate ndi malamulo Ake.

10. Mwachidule

Tawonetsetsa motsamala ku chokera mu Baibulo zomwe Mulungu amawulura zokhudzana za Iye mwini pachiyambi. Taphunzira kuti:

1. Kuti pali Mulungu m'odzi yekha woona wotchedwa Atate. Yohane 17:3; 1 Akolinto 8:6; 1 Timoteo 1:17
2. Iye ndiye gwero la moyo wonse ndi m'dalitso. Yakobo 1:17
3. Anabweretsa Mwana Wake muchifanidziro chake ndipo anamupasa Iye mphamvu zonse ndi kumupanga Iye kufanana naye. Ahebri 1:1-5 Miyambo 8:12-30; Afilipi 2:6; Yohane 5:26; 8:42; Akolose 2:9
4. Mwana wa Mulungu ndi mfungulo wa ufumu wa Mulungu. Iye ali ndi makhalidwe wokhulupirika womvera ndi wogonjera ndi m'dalitso. Mateyu 3:17; Masalimo 40:8; Yohane 8:29
5. Mzimu wa Mwana umatsefukira ku chirengedwe ndi kukhala m'mitima mwa onse amene asankha kugongera ku malamulo a Atate. Chivumbulutso 22:1, 2; Yohane 7:37, 38; Aoma 8:9, 10
6. Lusifala, mngelo woyamba kulengedwa, anakana chindikiro cha Mwana wa Mulungu ndipo anakana kugonjera ku lamulo la Mulungu lopembedza Iye. Yohane 5:22; Afilipi 2:6; Chivumbulutso 12:7-9; Ahebri 1:6
7. Lusifala anakhala Satana ndikutenga gawo limodzi la atatu la angelo ndi iye muchikhulupiro chatsopano chakuti sipafunikira kugonjera Mulungu chifukwa ali ndi moyo wawo mwa iwo eni. Chivumbulutso 12: 4; Gen 3:4,5
8. Kukana malamulo a Mulungu zikufanana kupha Mwana Wake - kugonjera kwenikweni, kudalira ndi kumvera. Yohane 8:44; Chivumbulutso 13:8; 1 Yohane 3:15
9. Mwana anagonjera ku dongosolo la Atate Ake kuwonetsa chirengedwe momwe kukana Iye kwenikweni kumachitira kwa Mwana Wake, potumiza Iye kuzatifera ife. Genesis 3:15; Ahebri 6:6

Tsopano takupasani kuchokera mu Baibulo chithunzithunzi cha Mulungu, Mwana wake ndi Mzimu wawo, ndi momwe amagwirira ntchito. Taphunziranso za bodza la Satana kukhuzana kumene kumachokera moyo ndi mzimu wake wokana. Tsopano tiyeni tifufuze chiyambi cha njira za machitidwe awiriwa amene anatuluka pa dzikoli.

11. Njira ziwiri

Mitu yambuyoyi, tinawonetsetsa kutsiyana kwakukula mu maganizo pakati pa Mulungu ndi Satana.

- Ufumu wa Mulungu unakhadzikisidwa posindika kupatulika kwa maubale ; ufumu wa Satana umatsamira pakupeza ndi kukhala ndi mphamvu.
- Ufumu wa Mulungu umagwira kupyolera m'dalitso pogonjera, kudalira ndi kumvera; ufumu wa Satana umagwira kupyolera m'dalitso lokana ndi pozidalira popanda ulamuliro wa Mulungu.
- Ufumu wa Mulungu umafotokoza za kufanana ndi kuthekera kodziwa wina; ufumu wa Satana umafotokoza za kufanana ndi kuthekera, udindo ndi kupambana kupyolera mphamvu zachibadwa.
- Ufumu wa Mulungu umayendetsedwa kupyolera kupangidwa kwa banja ndipo onse aufumu amakakamizidwa ndi chikondi; ufumu wa Satana umalamulidwa kupyolera kupangidwa kwa mphamvu zotsiyansiyana ndipo okhalamo amakakamizidwa ndi nkhanza.
- Ufumu wa Mulungu umafotokozedwa za phindu la khalidwe ndi ubale; ufumu wa Satana umafotokozedwa za phindu la mphamvu.

Kutsiyanaku onani mwachidule m'mavesi amu Baibulo motere:

Yeremiya 9:23-24 Atero Yehova, wanzeru asadzitamandire m'nzeru zace, wamphamvu asadzitamandire m'mphamvu yace, wacuma asadzitamandire m'cuma cace; koma wakudzitamandira adzitamandire adzikweze umo, kuti ali wa kuzindikira, ndi kundidziwa Ine, kuti ndine Yehova wakucita zokoma mtima, ciweruziro, ndi cilungamo m'dziko la pansu, pakuti m'menemo ndikondwerera, ati Yehova.

Pamene tifufudza mbiri, tidzawona kuti maganizo a anthu a amuna za Mulungu ndi ogawanikana pa njirazi. Nthawi zina zikhoza kukhala zovuta kuzindikira kuti ndi njira iti chifukwa ufumu wa Satana nawonso umagwiritsa maubale ndi cholinga chopeza mphamvu choncho mayankhulidwe angamveke ngati ndi aubale ndithu pamene cholinga ndi chapa mphamvu basi.

Pamene Satana ankathanthauzira kwa Eva, kuvomera chikhulupiriro kuti tiri ndi moyo mwa ife tokha timatsogozedwa mwachikhalidwe kudziona tokha ngati milungu. Ndikudzindikiraku, maganizo a anthu ambiri a Mulungu ali

ngati makhalidwe ndi kuthekera kwa anthu. Izi zikuwoneka kwambiri mu nthano zaku Herene (Greece) ndi kufotokoza kwa Zeus - kalonga wa milungu; Aphrodite - mulungu wa chikondi ndi kukongola; Apollo - mulungu wa nyimbo, mankhwala, thanzi; Ares - mulungu wa nkhondo. Milunguyi ndi makhalidwe a anthu basi ndikuti kwenikweni ndi kuzipembeza okha ndi iwo eni milungu, m'mene anamulonjezera Eva m'munda wa Edeni.

Ndikufuna ndiyambe za mbiri pofanidzira anthu awiri m'Baibulo omwe amafotokoza momveka bwino za njira ziwiri: Abrahamu ndi Nimurodi.

12. Chiyambi cha Babulo

Tisanayambe kufotokozera nkhani ya Abrahamu ndi Nimurodi, tiyamba kuwunika mbiri yofikira ku nthawiyi .

Chipatso choyambirira cholandira bodza mwa Satana chinali matha. Wonani:

Genesis 3:9-10 Ndipo Yehova Mulungu anaitana mwamunayo nati kwa iye, Uli kuti? Ndipo anati, ndinamva mau anu m'mundamu, ndipo ndinaopa cifukwa ndinali wamarisece ine; ndipo ndinabisala.

Kuchokera pamene Adamu analandira bodza, adakhulupirira kuti munali moyo mwa iye yekha. Bvuto linali lakuti tsopano anadzindikira kuti Mulungu anali gwero lalikulu ndi wa mphabvu pa moyo kuposa iyeyo. Idzi zinadzetsa matha. Pamene Adamu sadakhulupira poyamba za moyo mwa iye yekha ndi wokondwa kudalira kuti Mulungu anali Atate wa chikondi womupatsa iye chiri chonse - palibe matha ngati amenewo kuwatsekerera. Chipatso choyamba cha bodza ndi MANTHA.

Chotsatira china chimene bodza linapanga chinali KUNYADA. Pamene Adamu adafunsidwa zomwe adachita, sadavomeredze kuti analakwa. Kunyada kwake sikunamulore iye kutero.

Genesis 3:11-12 Ndipo anati, Ndani anakuuza iwe kuti uli wamarisece? Kodi wadya za mtengo uja, umene ndinakuuza iwe kuti usadye? Ndipo anati mwamunayo, Mkazi amene munandipatsa ine kuti akhale ndi ine, ameneyo anandipatsa ine za mtengo, ndipo ndinadya.

Adamu ananeneza mkazi wake. Akanakumbukira kuti mu njira ya Mulungu iyeyo ndi mutu wa banja; udindo onse udali m'manja mwake pa zonse zochitika mu banja lake. Pomuneneza mkazi wake anapereka bodza kuti iye anakhulupirira kuti mkazi wake adali ndi mphamvu mukati mwake kuti zimusokonedze chikhalidwe chake, choncho iye atha kuneneza mkaziyo ndikusatenga udindo. Ndizoveka kuti Eva adamuyetsa Adamu, koma adachita chisankho chake yekha choncho anali ndi udindo. Koma sadavomeredze ichi. Ichi ndi chipatso chachiwiri cha bodza - KUNYADA.

Zipatso ziwirizi zidakhadzikitsa mbeu ya kudzuka kwa Babulo. Zipatso zoyipa zambiri zikanabwera. Adamu ndi Eva anavomereza kulakwa kwawo, koma mbeu za kupanduka zinakhazikika ndipo iwo napasira kwa ana awo Kaini ndi Abel. Abel ananyadira kugonjera Mzimu wa Kristu ndi mozichepetsa anatsatira dongosolo la Mulungu lo bwezeretsa mtundu wa anthu kulandiranso mwathunthu Mwana Wake. Kaini anavomereza Mulungu koma

anakana kusatira dongosolo la Mulungu. Pano pali chipatso chachitatu - KUKANA. Adasitha njira yake ya mapemphero kumuyenera iye ndikunyalanyaza nsembe ya nkhosa. Abelo anadandaulira m'bale wake kuchita monga adawonetsedwera , koma Kaini anakana kumvera. Kaini adapitirira kukana ndipo Satana anamupangisa iye mwankhaza kupha m'bale mwake m'mkwiyo. Pano pali zipatso zambiri : MKWIYO, UDANI NDI KUPHA. Kuphedwa kwa Abelo ndikufotokozera za mtima wa Satana kwa Kristu. Waulemu wogonjera Abelo anaphedwa ndi m'bale wake wouziridwa ndi Satana ngati umboni woyamba wa maganizo achiwawa kwa Kristu amene anabisika m'mtima wa Satana.

Monga tatchulilra poyamba, mzimu wokana umatichosera ife m'lingaliro wa m'dalitso ndi kuvomerezeka kwa Mulungu. Popanda m'dalitso wa Mulungu ife timamva osatetezeka ndi achabechabe. Kaini anakana kudandaulira kwa makolo ake kwa iye, anakana kudandaulira kwa m'bale wake Abelo ndiponso anakana kudandaulira kwa Mulungu kwa iye. Kukana kwambiri kwa Kaini kunakhala, kunamutsatira kwambiri wosatetezeka ndi wachabechabe. Pamene Mulungu adalengedza temberero pa Kaini, ichi sichithu chimene Mulungu amachiyika pa iye, koma izi mwachirengedwe ndi zotsatira za kukana lye; MATHA, OSATETEDZEKA NDI WACHABECHABE. Tembereroli mwa chirengedwe nzotsatira za zochita za Kaini - Mulungu anangochivomereza.

Genesis 4:11-12 Tsopano ndiwe wotembereredwa kunthaka, Imene inatsegula pakamwa pace kulandira pa dzanja lako mwazi wa mphwako: pamene udzalima panthaka siidzaperekanso kwa iwe mphamvu yace: udzakhala wothawathawa ndi woyendayenda pa dziko lapansi.

Mau woti wothawathawa ndi woyendayenda akupereka m'lingaliro woyendayenda, wokayikakayika, ndi kusakhazikika. Izi ndi zipatso zopitirira: OSATETEZEKA, KUSAKHAZIKIKA NDI WACHABECHABE.

Pamene Adamu ndi Eva anatataya Abelo, Mulungu adawapatsanso Mwana wina wa mwamuna - Seti. Iye anawonetsera kwambiri mzimu womwewo wozichepetsa wa Adamu ndi Abelo. Choncho mafuko awiri anatuluka kuchokera mu banja la Adamu; fuko la Seti, limene, lodzadzidwa ndi m'lingaliro wa m'dalitso wa Atate pogonjera ku malamulo Ake anatchedwa

ana amuna a Mulungu ndipo fuko la Kaini, limene, lodzadzidwa ndi zipatso za kupanduka ndi wachabechabe anatchedwa ana a amuna ndi a akazi a anthu.

Satana adadziwa kuti chifukwa Mulungu adakonzā ubale wa anthu m'mabanja, kuti ana obadwa mu dziko kwambiri amadalira makolo awo. Chikhalidwechi chitha kuthandiza ana kuphunzira kudalira pa Mulungu. Munthu wofunikira kwambiri m'banja kuphunzitsa ana khalidwe la mtengo wapatali wogonjera anali mai. Satana anayesa ana a Mulungu kufuna ana a akazi a anthu kuwawatira iwo. Ana a Kaini anali wodzadzidwa ndi mzimu wa atate awo: mantha, kunyada, kupanduka, m'kwiyo, ndi udani. Zipatso zonsezi zinabisika m'mitima ya azimai amene anaphunzira kupanga mawonekedwe awo a kunja kukhala wokongola. Ana a amuna a Mulungu sanadzindikire makhalidwe awo ndipo anakwatira azimaiwa. Migwirizanoyi yinatsogolera ku nkhaza zoipa kwambiri. Baibulo limawatcha iwo zimphona; tanthauzo ndilo mofananira kuti zimphona zodzikuza zofuna kupeza mphamvu.

Genesis 6:1-5 Ndipo panali pamene anthu anayamba kuculuka padziko, ndi ana akazi anawabadwira iwo, kuti ana amuna a Mulungu anayan'gana ana akazi a anthu, kuti iwo anali okongola; ndipo anadzitengera okha akazi onse amene anawasankha. Ndipo anati Yehova, mzimu wanga sudzakangana ndi anthu nthawi zonse, cifukwa iwonso ndiwo thupi lanyama: koma masiku ace adzakhala zaka zana limodzi kudza makami awiri. Pa dziko lapansi panali anthu akulukulu masiku omwewo ndiponso pambuyo pake, ana amuna a Mulungu atalowa kwa ana akazi a anthu, ndipo anabalira iwo ana, amenewo ndiwo anthu amphamvu akalekale, anthu omwe. Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukulu pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha.

M'kanthawi kochepe, Mzimu wa Yesu wokonda kugonjera unachotsedwa m'mitima mwa ana a Mulungu ndikuti maganizo a pafupifupi onse anali oyipa kosalekeza. Mulungu anachotsa Mzimu Wake ndikulola chigumula chiretse zoipa, kuwonongedwa ndi chiwawa. Iye anafikira mphulupulu za atate pa ana m'pakana m'bandwo wachitatu ndi wachinai. Mulungu anayambanso ndi Nowa ndi banja lake koma posachedwa Satana anapeza polowera kuzera mwa Hamu kukhazikitsa maziko a ufumu wa Babulo. Hamu anatengeka ndi anthu oipa a m'dziko lakale. Tsiku lina pamene iye anapeza atate ake mu hema mwao, maliseche ndi oledzera, iye anaasokoneza iwo ndipo anawapanga china chake choyansa kwambiri moti chipatso cha uchabechabe, kusatetezedwa ndi kupanduka zipange zizukulu zake ziyeye

misanje yatsopano ya ulamuliro, azilamulira ndi zoipa za misanje yawo yosatetezedwa ndi mantha.

Nimrode anali chizukulu cha Hamu. Baibulo likutero za iye:

Genesis 10:8-10 Ndipo Kusi anabala Nimrode; ndipo iye anayamba kukhala wamphamvu pa dziko lapansi. Iye ndiye mpalu wamphamvu pamaso pa Yehova: cifukwa cake kunanenedwa, monga Nimrode mpalu wamphamvu pamaso pa Yehova. Ndipo kuyamba kwake kwa ufumu wake kunali Babele, ndi Ereke, ndi Akadi, ndi Kaline, m'dziko la Sinara.

Mawu akuti wamphamvu atathauza mphamvu zankanza. Panalibe kugonjera mwa Nimrode. Iye ndi munthu woyambirira mu Baibulo amene anaganizidwa udindo wa Mfumu, ndikufotokozedwa kuti anamanga ufumu wake popanda kuzindikira Mulungu Wakumwamba. Mzinda woyamba mu ufumu wake unali Babele kapena kuti Babulo. Tsopano poti tayala maziko a khalidwe la Nimrode, tingaone zinthu za chipembedzo chimene iye anakhazikitsa.

Ngati mufuna kudziwa zambiri mukhodza kudzipedza pa makina a intaneti mu buku lotchedwa *life matters* kuchokera ku maranathamedia.com/book/view/life-matters.

13. Zochitika mu Babulo

Tikati tiganizire zinthu zovuta zimene zinapanga khalidwe la Nimrode, titha kulingalira mtundu wa dongosolo la chipembezo chimene anga khazikitse. M'mzimu wakukana, chitha kukhala china chake chotsutsana ndi m'mene Baibulo limaululira za Mulungu ndi ndendende m'mene Nimrode anakhazikitsira. Pano pali mau amene kaswiri wina wolemba mbiri Josephus anafotokozerera za maziko a nzeru za Nimrode:

“Tsopano anali Nimrode amene anasonkhezera iwo kunyoza Mulungu. Iye anali chizukulu cha Hamu, mwana wa Nowa, munthu olimba mtima, ndi wadzanja la mphamvu kwambiri. Iye anakopa iwo kuti asanenere mphamvuzo kwa Mulungu, monga ngati kuzera mwa iye iwo anali okondwa, koma kukhulupira choncho zinali ngati ndi kuzera m'mtima wao wolimba anapezera chimwemwe. Iye pang'ono ndi pang'ono anasintha boma kukhala la nkhanza, anthu osawona njira ina kutembenukira kukuopa Mulungu, koma kuwabweretsa iwo kudalira pa mphamvu yake....” Josephus. Antiquities Book 1 Chapter 4 Para. 2

Nimrode mwamphamvu anakana m'dalitso wa Mulungu posankha bodza la njoka. Iye anasankha kukhazikika pa mphamvu m'malo mwa khalidwe. Anaphunzitsa anthu kuziwona mwa iwo okha monga m'mene adawaphunzitsira Adamu ndi Eva. Nzeruyi itha kukhuza kwambiri dongosolo la banja. Onani momwe wina wolemba mbiri akunenera:

“Ulamuliro wa olamulira akale umasamira pa kumverera abale, ndipo kulamulira kwa mtsoleri chinali chifanizo cha kulamulira kwa makolo. Nimrode, mosiyana, anali wolamulira mwayekha m'gawo, ndikuti anthu ngati akukhalamo alamulidwa osawerengera maubale awo. M'mbuyomu munali mafuko - maanja aakulu - gulu la anthu; tsopano panli dziko, gulu la ndale - boma...” A.T.Jones. Empires of the Bible. 1904 Page 51

Mibadwo ya kalero imatumikira ndi kulimbikitsa kuti ndondomeko ya m'dalitso kuzera pomvera ku banja lolamulidwa ndi bambo ndilosamalidwa ndi mai. Nimrode anasintha zonsezi ndikupanga podalira pa mtsoleri wa dera lake wokhala ndi zinthu zowoneka monga mbewu, malo ndi nyumba. Mabanja anali oyendayenda ndipo amalamulinda m'mafuko awo. Ulamuliro unakhazikika pa kupereka ulemu ku ubale. Nimrode analamulira kuzera kuwopa mphamvu ndi kupanga anthu kumutumikira iye mwa nkhanza.

Nimrode anapitiriza kuphwanya chifanizo cha Mulungu mu ubale wa mwamuna ndi mkazi. Nimurodi anakwatira a mai ake. Ubale m'ukwati wa m'khalidwewu ndi wosiyana kwambiri ndi ubale wa Atate ndi Mwana mungapeze.

Pamene Nimrode anamwalira, mkazi wake amene anali amai ake Semiramisi ananena kuti Nimrode tsopano waphatikizidwa mu dzuwa ndikuti ali wowatetezera ndiwowasamalira. Semiramisi tsopano anakhala mukhala pakati wa moyo wathupiri padzikoli ndi moyo wauzimu kumwamba. Umu ndi m'mene anapezera udindo wa "Mfumukazi ya Kumwamba".

Yeremiya 7:18 Ana atola nkhu, atate akoleza moto, akazi akanyanga ufa, kuti aumbe mikate ya mfumu yaikazi ya kumwamba, athirire milungu yina nsembe yothira, kuti autse mkwiyo wanga.

Kulumikizana ndi iye inali njira yopezera chitetezo ndi mphamvu za Nimrode. Chipembezochi chinafalikira ndi chipembezo cha dzuwa chinakhazikika mbali zambiri zotchedwa dziko nthawi yimeneyo. Tsiku la dzuwa (Sun-day) linakhala tsiku lapamwamba kwambiri lamapemphero kususana ndi m'dalitso wapadera wa Mwana wa Mulungu wobwera m'maola a Sabata.

Genesis 2:3 Tsiku lacisanu ndi ciwiri Mulungu anamariza ntchito yonse anaipanga; ndipo anapuma tsiku lacisanu ndi ciwiri ku ntchito yace yonse.

Semiramisi anali ndi mwana wamwamuna wotchedwa Tamuzi. Kuteteza udindo wake, iye anati anabereka mwanayo kuchokera polumikizana ndi kunyezimira kwa mphamvu ya dzuwa - Nimrode. Nimrode tsopano anabadwanso mwa Tamuzi. Kubadwansoku kunakhala kolumikizana ndi kusinthika kwa nthawi ya mvula ndi kupembeza chirengedwe. Chikondwerero cha kulira Tamuzi chinakhazikika panthawi yimene zomera zobiriwira za nthawi ya mvula ndi chirimwe ikutha. Chipembezochi chimafanizidwa ndi chifanizo cha (mai) Maddona atagwira mwana wake.

Ezekieli 8:14 Pamenepo anadza nane kucitseko ca cipata ca nyumba ya Yehova colozza kumpoto; ndipo taonani, apo panakhala akazi akulirira Tamuzi.

Kuzera mwa Semiramisi, chipunzitso cha kusafa kwa moyo kunakhazikika, umulungu wa munthu mu umunthu wa Nimrode, kupembeza mphamvu ndi miyambo yosiyanasina yobweretsa mvula ndi chonde zonse zinakhala mbali ya chinsinsi cha Babulo. Popeza Semiramisi anakhala njira yopezera

mphamvu ya Nimrode, mwambo unakhazikika wa mwamuna kulumikizana pogonana ndi mkazi kupeza mphamvuyo. Choncho kunatuluka m'chitidwe wachiwerewere m'kachisi, ndi kupembeza dzuwa ndikugonana ngati mbali ya utumiki wachipembezo. Sizitengera zambiri kuwona kuti popanda banja lozipereka mwamphamvu, chipembezo chithakuwoneka ngati chachikoka ku mtima wa thupi. Nfundo yofunikira kuti tipange ndiyoti pamene khumbo lofuna mphamvu likhala cholinga chathu kwambiri, zifanizo zeizeni za iwo amene tifunako sizikhalanso zofunikira. Chifanizo cha munthu nchofunikira pokha mu ubale m'mene muli maubale pakati pawo. Chipembezo cha Babulo chimazungulira pa ganizo la anthu atatu anali olumikizana mosadziwika. Chifukwa Nimrode anali mwana wa Semiramisi, komanso anali mwamuna wake ndi kepanako akuti anabadwanso kukhala Tamuzi, zifanizo za anthuwa zikukhala zimazimirira mu Mulungu modzi wosadziwika mwa anthu atatu. Monga tangonenera, kudziwa chifanizo chenicheni cha anthu sichofunikira pamene mphamvu ndizimene taganizira pa chipembezo chathu. Ichi nchosiyana kwambiri ndi chipembezo cha Mulungu wakumwamba. Nkwabwino kudziwa chifanizo cha Atate ndi Mwana kuti tipeze chimwemwe ndi m'dalitso wa ubale wawo. Zifanizo zawo zisasokonezeke, kuphatikizidwa kapena kupangidwa zosadziwika. Paliponse zichitika izi tisimikiza kuti ndi mulungu wamphamvu wopangidwa ndi Satana amene akupembezidwa, osati Atate ndi Mwana wamu Baibulo.

M'zonse m'mene ndachitira pandekha ndinso ena m'chi Kristu, ndapeza kusokonekera kwambiri amene akutchulidwa mundime zina mu Baiulo ndi amene timamuyankhula mu pemphero. Ndawona anthu kufotokoza mosokonekera nthawi zambiri kwa amene kwenikweni akumupemphera, ndipo posafuna kulakwa posiya m'modzi. Chisokonekerochi chimachokera ku zochitika za m'Babulo ndipo chimapereka kufuna mphamvu kusiyana ndi kufuna Atate ndi Mwana ndi khalidwe lawo. Izi zimachitika mosaziwa kwenekweni ku mbali ya ofunayo, koma zimene zimaphunzitsidwa zimaatsogolera iwo kuchisokonekerochi mosadziwa. M'chitidwe waku Babulo unapangidwa kungonena kwa ulemu ndi kukonda Mulungu; pamene kuona kwenikweni zimatanthauza kuyiwala lye ndi kuyika munthu m'malo mwa lye.

Pamene pali mbiri yambiri yimene titha kunena za chipembezo cha dzuwa chaku Babulo nfundo zofunikira tikufuna tiwone ndi nthanthi za maziko molingana ndi m'mene Baibulo limaululira za Mulungu. Chipembezo cha Nimrode, Semiramisi, Tamuzi chimakhazikika pa zotsatirazi:

1. Chikhulupiriro cha kusafa mwachibadwidwe
2. Mphamvu zochokera m’kati mwathu
3. Kukana Atate dongosolo Mutu/M’dalitso kukonda ubale Wolamulira/Wankhanza - Mai/Mwana
4. Maubale opotoka a m’banja
5. Womanga mizinda ndi kukhazikika pa kupeza madera ndi katundu.

Dongosololi ndikukwaniritsa kwa lonjezano la Satana loti munthu azakhala ngati milungu kudziwa zabwino ndi zoyipa. Chipembezo china chirichonso chokuphatikizapo m’khalidweu chiri ndi chikoka cha ufumu wa Satana mwakuya. Tikumbukire kuti chipembezochi nchochokera ku mantha, kunyada, kupanduka ndi kugonana kopotoka zimene ziri zosiyana kwambiri kwa Mulungu wofotokozedwa m’Baibulo.

14. Njira ya Mibadwo

Zikhodza kukhala zotithandiza kuwona njira zimene zinatsatiridwa ndi Nimrode ndi mabwenzi ake popanga maganizo awo za Mulungu. M'tumwi Paulo akusanthula mosalambalala za nthawiyo ndi zotsatira pa anthu. Tigwiritsa ntchito kusanthulaku ngati chimango cha kukambirana kwathu.

Pachiyambi Mulungu anapanga munthu m'chifaniziro Chake. Tinawona izi mu mutu woti Kupangidwa m'chifanizo Chake. Mbali ya chifukwa chimene Mulungu anamupangira munthu m'njirayi yinali yophunzitsa chirengedwe kupambana kwa ubale pakati pa Iye ndi Mwana Wake. Wonani m'mene Paulo akufotokozero:

Aroma 1:19-20 cifukwa codziwika ca Mulungu caonekera m'kati mwao; pakuti Mulungu anacionetsera kwa iwo. Pakuti cilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yake yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zithu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula:

Zikupanga m'lingaliro okwana kuti Satana mwachidunji angawonongera ubale pakati pa Mwamuna ndi Mkazi kulesa kuti chidziwitso cha Mulungu chitsamvetssetseke. Paulo akufufuza mbiri ya Nimrode mwachidule, titsatira izi mwandondomeko:

Aroma 1:21-25 cifukwa kuti, ngakhale anadziwa Mulungu, sanamcitira ulemu wakuyenera Mulungu, ndipo sanamyamika; koma anakhala opanda pace m'maganizo ao, ndipo unada mtima wao wopulukira, Pakunena kuti ali anzeru, anapusa; nasandutsa ulemelero wa Mulungu wosaonongeka, naufanizitsa ndi cifaniziro ca munthu woonongeka ndi ca mbalame, ndi ca nyama zoyendayenda, ndi ca zokwawa. Cifukwa cake Mulungu anawapereka iwo m'zilakolako za mitima yao, kuzonyansa, kucititsana matupi ao wina ndi mnzace zamanyazi; amenewo anasandutsa coonadi ca Mulungu cabodza napembedza, natumikira colengedwa, ndi kusiya Wolengayo, ndiye wolemekezeka nthawi yosatha. Amen.

Ngati chidzukululu cha Hamu, Nimrode amadziwa bwino lomwe za Mulungu wa kumwamba. Koma pomwe Nimrode analandira bodza kuti mphamvu sichokera kwa Mulungu koma m'kati mwathu, analeka kumulemekeza Mulungu kapena kuthokoza madalitso a Mulungu. Izi zidachititsa Nimrode ndi mabwenzi ake m'lingaliro labodza kapena kuti lachabe za zoti iwo ndani. Ntchito za mamuna ndi mkazi zomwe zidakhazikisidwa bwino ndi Mulungu

zinapotozedwerathu ndikusokonezeka ndi ngalande ya m'dalitso kuchokera kumwamba inaduka. Mzimu wokoma wogonjera wa Mwana wa Mulungu unaletsedwa kulowa m'nyumba zawo ndi mitima yawo inadetsedwa. Kutchedwa kumasulidwa kwa amayi ndi ufulu watsopano wogonana unawoneka ngati wapatsogolo ndi nzeru, koma zinawapanga iwo wopusa.

Tinawona kuti atangomwalira Nimrode, Semiramisi adafalitsa kuti Nimrode tsopano adali mulungu yemwe waphatikizidwa ku dzuwa. Ganizo la Mulungu limasithidwa m'chivundi cha munthu. Munthu anali m'chivundi m'lingaliri lake zoti moyo wake unachokera kuti ndi chifanizo cha umulungu cha ubale wa mwamuna ndi m'kazi anataya. Chipembezo chabodza zachikazi kupeza mphamvu za Nimrode, kubadwanso kwa Nimrode mwa Tamuzi ndipo choncho kupembeza chirengedwe zimene zimatanthauza mbalame, nyama za miyendo yinai ndi zokwawa zonse zimatumikira kuchotsa nkhope ya chifanizo cha Mulungu mwa munthu ndi kusintha choonadi cha Mulungu kukhala bodza.

Mulungu wa Babulo anali kwenikweni kupembeza ndi kufunafuna mphamvu. Monga tanenera poyamba, kufunafuna mphamvu kumasamalira pang'ono za kudziwika kwa wopembezedwa, khalidwe lawo ndilofunikira pang'ono kuyerekeza ndi mphamvu zawo. Kuphatikizana kwa chinsinsi kwa mayina a Nimrode, Semiramisi ndi Tamuzi kunakhuza kwambiri mayina a amuna ndi akazi ndi njira zawo zokhuzana ndi ubale wa wina ndi m'nzake. M'khalidwe wogonana unakhala wofunikira kwambiri kuposana ndi mayina ogwiritsidwamo, ndipo choimira chake chinatenga tanthauzo losiyana kwambiri.

Aroma 1:26-28 cifukwa ca ici Mulungu anawapereka iwo ku zilakolako za manyazi: pakuti angakhale akazi ao anasandutsa macitidwe ao a cibadwidwe akhale macitidwe osalingana ndi cibadwidwe: ndipo cimodzimodzinso amuna anasiya macitidwe a cibadwidwe ca akazi, natenthetsana ndi cholakalaka cao wina ndi mnzace, amuna okhaokha anacitirana camanyazi, ndipo analandira mwa iwo okha mphoto yakuyenera kulakwa kwao. Ndipo monga iwo anakana kukhala naye Mulungu m'cidziwitso cao, anawapereka Mulungu kumtima wokanika, kukacita zinthu zosayenera;

Kugonana amuna kapena akazi wokhawokha linali khalidwe lopitirira la chipembezo cha Babulo. Kugonana inakhala njira yolandirira mphamvu kuchokera kwa amene agwirizana nawo, monga taonera m'mlonda Semiramisi. Ziganizo za umutu ndi kugonjera tsopano zinali

zosagwirizananso. M'lingaliro la Baibulo la wamphongo ndi zachikazi zinatayidwa pofunafuna kuzipembeza ndi mphamvu. Paulo ndiyeno akufotokoza zotsatira zake:

Aroma 1:29-32 anadzala ndi zosalungama zonse, kuipa, kusirira, dumbo; odzala ndi kaduka, mbanda, ndeu, cinyengo, udani; akazitape, osinjirira, akumuda Mulungu, achipongwe, odzitama, amatukutuku, oyamba zoipa, osamvera akulu ao, opanda nzeru, osasunga mapangano, opanda cikondi ca cibadwidwe, opanda cifundo; amene ngakhale adziwa kuweruza kwace kwa Mulungu, kuti iwo amene acita zotere ayenera imfa, azicita iwo okha, ndiponso avomerezana ndi iwo akuzicita.

Anthu akudabwa chifukwa ninji kuli chiwawa chambiri, kudana ndi chiwerewere m'dziko lapansi! Aroma woyamba akuwonetsera poyera chifukwa ndi momwe zimayendera moteremo. Ndiye mwachidule ndondomeko yake motere:

1. Kuyiwala kuti zonse moyo ndi m'dalitso zichokera kwa Atate ndi Mwana
2. Chikhulupiro kuti munthu mwachibadwidwe ali ndi gwero la moyo
3. Kuwonongeka kwa m'gwirizano wa banja kumene kumateteza umutu ndi mfundo ya m'dalitso mogonjera
4. Kupotoka kwa kugonana
5. Kulimbikitsa maganizo achabechabe, mantha, kunyada, m'kwiyo, udani, ndi kupha chifukwa chosowa m'dalitso
6. Ziyerekezo za ubale wachinyengo kwa Mulungu: kutanthauza kusawona bwinobwino mayina ndi kupembeza mphamvu kuposa khalidwe.

Ndondomeko iyi ndiyotengedwa mu Babulo. Lingaliro la Baibulo la Babulo ndi lakuya kwambiri kuposa ufumu wowoneka ndi maso. Zimayimira kuukira moopsyia ndi chiwawa kwambiri pa malingaliro a munthu chimene chimachitika. Mphamvu yake ndiyoyika malingaliro pa ukapolo mowoopsyia kwambiri. Kugwira mozembaku nkodesa nkhwawa. Njira ndi mitundu yogwirira ntchito ndizobwezedwa. Mphamvu za maunyolo ake ngovuta kudula ukangotengedwa ukapolo - pokhapokha...

Pokhapokha titaphunzira mbiri ya Abrahamu. Mbiri yake imapereka nkhani yofunikira kwambiri yothawira Babulo. Abrahamu anachokera ku dziko la Babulo, banja lake linakhuzidwa mu chipembezo cha Babulo, koma iye

anathawa. Nkofunikira kwambiri m'mene Paulo akuyambira kalata yake kwa Aroma kuyankhula za mphamvu ya Mulungu mu uthenga wabwino kenako tsatanetsatane m'ndondomeko m'moyo wa Abrahamu.

Aroma 1:16-18 Pakuti uthenga wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu aliyetse wakukhulupirira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene. Pakuti m'menemo caonetsedwa cilungamo ca Mulungu cakucokera kucikhulupiriro kuloza kucikhulupiriro: monga kwalembedwa, Koma munthu wolungama adzakhala ndi moyo ndi cikhulupiriro. Pakuti mkwiyo wa Mulungu, wocokera kumwamba, uonekera pa cisapembedzo conse ndi cosalungama ca anthu, amene akanikiza pansa coonadi m'cosalungama cao;

Aroma 4:16-21 Cifukwa cace cilungamo cicokera m'cikhulupiriro, kuti cikhale monga mwa cisomo; kuti lonjezo likhale lokhazikikakwa mbeu zonse; si kwa iwo a cilamulo okhaokha, koma kwa iwonso a cikhulupiriro ca Abrahamu; ndiye kholo la ife tonse; monga kwalembedwa: Ndinakukhazika iwe kholo la mitundu yambiri ya anthu pamaso pa Mulungu amene iye anamkhulupira, amene apatsa akufa moyo, ndi kuitana zithu zoti palibe, monga ngati zilipo. Amene anakhulupirira nayembekeza zosayembekezeka, kuti iye akakhale kholo la mitundu yambiri ya anthu, monga mwa conenedwaci, mbeu yako idzakhala yotere. Ndipo iye osafooka m'cikhulupiriro sanalabadira thupi lake, ndilo longwa ngati lakufa pamene, (pokhala iye ngati zaka makumi khumi), ndi mimba ya Sara idaumanso; ndipo poyang'anira lonjezo la Mulungu sanagwedezeka cifukwa ca kusakhulupirira, koma analimbika m'cikhulupiriro, napatsa Mulungu ulemu, nakhadzikikaso m'mtima kuti, cimene Iye analonjeza, anali nayonso mphamvu yakucicita.

Mbiri ya Abrahamu kuthawa kuchokera ku Babulo ndi mtima weniweni wa uthenga wabwino wa Khristu; ndi mbiriyi titembenukira kenako kuti tiphunzire ndondomeko yosinthira ndondomeko zisanu ndi imodzi (6) - tatchula m'mwambamu -, kudula maunyolo a Babulo ndi kufuula "Babulo Wagwa!"

15. Kuyitanidwa kutuluka mu Babulo

Chipembezo chachinsinsi cha mafano chaku Babulo chinakhala pafupifupi cha dziko lonse. Baibulo likuti:

Yeremiya 51:7 Babulo wakhala cikho cagolidi m'dzanja la Yehova, amene analedzeretsa dziko lonse lapansi; amitundu amwa vinyo wake; cifukwa cace amitundu ali ndi misala.

Vinyo wa Babulo ndi ziphunzitso zake zonyenga zachinsisi zokhuza Mulungu zimene zimasokoneza malingaliro monga ngati wolezera. Ziphunzitsozi zimaononga maanja, kudula m'dalitso wa Atate a Kumwamba, ndi kupanga m'lingaliro wachabechabe, m'kwiyo, osatetezeka, kuphatikizapo kufuna kwambiri mphamvu.

Chikoka cha Babulo chinali kusintha maanja amene samakhala malo amodzi koma oyendayenda monga mafuko nkukhala malo amodzi a akulu ngati mizinda wotetedwa ndi asirikali. Midzi yaying'ono kusaduka mizinda yayikulu yokhala ndi malinga kuphwekesa chitetedzo. Misonkho inakhazikitsidwa kuti apereke chakudya ndi zida kwa asirikali. Misonkho imafunika kwa maboma olamulidwa ndi mafumu ankhanza kuti misonkhoyi isokhanitsidwe. Kuphana pafupipafupi kunaumitsa amuna poonjezera kukhala kutali ndi maanja awo kuphatikizana ndi chipembezo cha chiwerewere chinawatsogolera ku kwera kwa uhule kwambiri, kuwononga migwirizano ya banja ndi kuwapanga azimai wosawerengedwa ngati ng'ombe, pokhapo iwo akhale mahule amu kachisi kuti asalidwe bwino.

Ndondomekoyi inali m'mbali zambiri za madongosolo a Satana woononga fanizo la Mulungu m'munthu, kumuchotsera ulemu wake ndikumupanga kapolo wa zolinga zake pochita nkhondo ndi Mulungu. Mulungu anayankha ndi chikondi mwachifundo ndikumuyitana munthu kuti atulukemo ndikumanga ufumu wapa banja wosamira pa ntchito ya bambo yodalitsa ndikubwezeretsanso khalidwe la mtengo wapatali kwambiri - chisamaliro chogonjera cha mkazi kuphunzitsa mutundu wobwera momwe angagonjere kwa Atate Wakumwamba ndi Mwana. Abrahamu, kapena kuti Abramu monga iye anatchedwera poyamba, anakhala nthawi ya Nimrode itapita pang'ono komabe umboni wina ukuwonetsa kuti miyoyo yawo inatengera, pamene chipembezo cha Babulo chimalamulira mbali zambiri za dziko lapansi.

Genesis 12:1-3 Ndipo Yehova anati kwa Abramu, Turuka iwe m'ziko lako, ndi kwa abale ako, ndi kunyumba ya atate wako, kunka ku dziko

limene ndizakusonyeza iwe; ndipo ndidzakuyesa iwe mtundu waukulu, ndipo ndidzakudalitsa iwe, ndi kubukitsa dzina lako; nukhale iwe mdalitso; ndipo ndidzadalitsa amene adalitsa iwe; ndi kutemberere iye amene akutemberera iwe; ndip mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a dziko lapansi,

Malo omwe Abramam anayenera kuchoka anli pakati penipeni pa ulamuliro wa Nimrode, Akaldeya.

Genesis 11:26-28 Ndipo Tera anakhala ndi moyo zaka makumi asanu ndi awiri, nabala Abramam, ndi Nahori ndi Harani. Mibadwo ya Tera ndi iyi: Tera anabala Abramam, ndi Nahori, ndi Harani; ndipo Harani anabala Loti. Ndipo anafa Harani pamaso pa atate wake Tera m'dziko la kubadwa kwake, m'Uri wa kwa Akaldayo.

Mulungu adatenga Abramam kumuchotsa ku mudzi kwawo komwe adakulirako ndikudula mayanjano ndi mapembezedwe anawazolowera. Mulungu anatero kumudalitsa Abramam ndi chidziwitso cha ufumu wa banja wokhazikika pa ubale wa Atate ndi Mwana. Mulungu anachedwetsa kuthekera kwa Sara kukhala ndi mwana kufikira iwo awiri ataphunzira bwino lomwe za ubalewo.

Mulungu adamupanga Abramam kukhala dalitso pomukhazikitsa iye chitsanzo momwe banja liyenera kukhalira. Onse amene anatengera khalidwe la banja la Abramam ndi Sara anapeza mfunguro wolandirira m'dalitso wa Atate wa Kumwamba m'mitima mwawo ndikuwapatsanso m'lingaliro wolimba kuti iwo ndiwokonedwa momwe aliri osati chifukwa cha mphamvu ali nazo. Ufumu waukulu wolonjezedwa kwa Abramam unali ndi makonzedwe kwenikweni a kapangidwe ka banja.

Genesis 18:18-19 Pakuti Abrahamu adzakhala ndithu wamkuru ndi wamphamvu, ndipo mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsika mwa iye? Chifukwa ndamdziwa iye kuti alamulire ana ake ndi banja la pambuyo pake, kuti asunge njira ya Yehova, kuchita chilungamo ndi chiweruziro, kuti Yehova akamtengere Abrahamu chomwe anamunenera iye.

Mau akuti "Poti ndamudziwa iye" akupereka m'lingaliro wa ubale wapa mtima pakati pa Mulungu ndi Abrahamu monga Mulungu anamuphunzitsira iye momwe angatsamalire mkazi wake ndi ana. Anamufotokzera iye kuti zinapangidwa kuchokera pachiyambi za mwamuna ndi Tate kukhala ngalande ya Atate aku Kumwamba kutsanulira m'dalitso Wake chifukwa

chokondwera ndi iwo. Osati kokha kuti mwamuna ndi Tate anapasidwa mbewu m'thupi yoti yisamalidwe ndi mkazi wake kubereka ana, komanso iye anapasidwa mbewu m'uzimu kupereka kwa mkazi wake m'lingaliro woyamika ndi chikondi ndi ana m'lingaliro wa cholinga ndi phindu. Mverani zomwe Miyambo akunena za ichi:

Miyambo 17:6 Zidzukuluni ndizo korona wa okalamba; Ndipo ulemmerero wa ana ndiwo atate ao.

Kuthekera kwa Abrahamu kudalitsa mkazi wake ndi ana kunadalira kwambiri pa mzimu wogonjera wa Sara; ulamuliro wake unali waukulu pokhapokha m'mene iye anamupasira iye. Pomwe iye amapempherera kwambiri za utsogoleri wa mwamuna wake ndi kudalira Mulungu akanadalitsa iye ndi mau woyenera ndi chisankho ndi kugonjera ndi kudalira mau a mwamuna wake, kwambirinso ana ake akanawona kuti chomwe amanena chinali chofunika kwambiri. Ana amawona kwa a mai awo momwe mau a atate awo aliri wofunikira ndi mphamvu. Mtumwi Paulo akutiya ife momwe Sara anaphunzirira momwe akawonera mwamuna wake.

1 Petro 3:5, 6 Pakuti koteronso kale akazi oyera mtima, akuyembekezera Mulungu, anadzikometsera okha, namvera amuna ao a iwo okha, monga Sara anamvera Abrahamu, namuca iye mbuye; ameneyo mukhala ana ake ngati mucita bwino, osaopa coopsa cirri cose.

Popeza Abrahamu ndi Sara anachokera ku Babulo iwo anali ndi zambiri zoti aphonzi. Onse amapanga zolakwa pa njirayo zimene zinachedwetsa kwambiri Sara kubereka Isake. Patapita mayeso ndi maphunziro ambiri, Abrahamu ndi Sara analola Mulungu kudalitsa Isake kwambiri ndi Mzimu wa Mwana Wake kuti Isake anali olola kugonjera mpaka ifa monga Yesu analola pa mtanda. Abrahamu nayenso anaphunzira kuyamikira mzimu wogonjera kudziwa kudalira Mulungu ngakhale zimawoneka zosatheka kutero.

Genesis 22:1, 2, 10-12 Ndipo panali zitapita zimenezo, Mulungu anamuyesa Abrahamu nati kwa iye, Abrahamu; ndipo anati, Ndine pano. Ndipo anati, Tengatu mwana wako, wamwamuna wayekhayo, Isake, amene ukondana naye, numuke ku dziko la Moriya; numpereke iye kumeneko nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri lomwe ndidzakuza iwe.. Ndipo Abrahamu anatambasula dzanja lake, natenga mpeni kuti amuphe mwana wace. Koma mthenga wa Yehova anamuitana iye ndi mauodzera kumwamba, nati, Abrahamu, Abrahamu ndi iye anati, Ndine pano. Ndipo mthenga anati, usaika dzanja lako pa

mwana, usamcitire iye kanthu; cifukwa tsopano ndidziwa kuti iwe umuona Mulungu wako, pakuti sunandikanize ine mwana wako, mwana wako wayekha.

Ndizodabwitsa kuganizira kuti mu nthawi ya moyo wa munthu m'modzi Mulungu anatha kuwononga mchitidwe uchititsa ukapolo wa Babulo kuchokera mu malingalira ake ndi kubwezeretsa chipembezo cha Mulungu woona wa Kumwamba. Ulendo wa Abrahamu kuchokera ku Babulo ndi maziko a ulendo wathu lero. Mulungu woona waku Mwamba ndi Mwana Wake akuti yitana ife kuchoka ku milungu yonama ya dziko lapansiri kubwera mu ufumu wa ubale wa banja kumene phindu lathu libwera kuchokera ku ubale wa mabanja athu osati kuchokera ku zinthu tizipeza.

Mfundo ziri m'kabukuka zafotokozedwa modzama m'buku la Moyo Ngofunika (*Life Matters*) kuchokera pa tsamba la internet *maranathamedia.com*. Chonde pezani bukuli kuti mupeze kufotokozera mwakuya m'dalitso wa banja umene umagonjetsa ufumu wa Satana pongozera pokhala ndi chidziwitso cholondola cha Mulungu ndi Mwana Wake.



Nzeru Ya Mulungu

Yemwe ali ndi Mwana mwa iye alinso ndi moyo. Kodi izi zili chomwechi bwanji? Mwa Mwana wa Mulungu muli mtima moyera omwe uli womvera Atate ake. Nthawi zonse amapanga zosangalatsa Atate ake. Komanso ali ndi mdalitso wa Atate ake ndi kukhunzika ndichikondi. Mtima wa Mwana ndiwokhazikika m'chikondi cha Atate ake.

Ndi nzeru ya Atate kugawana Mzimu wa chikondi cha Mwana wake wokonedwa ku chilengedwe chonse; kukoma, kudekha ndi Mzimu omvera wokonda malamuro a Atate ake. Khristu ndi nzeru ya Mulungu ndi chitetezo chachikondi mu ufumu wa ubale.

Mzimu wozichepetsawu umasefukira kuchokera ku mpando wa Mulungu kutsikira kupyorera mtengo wa moyo. Satana anakana Mwana wa Mulungu ndi Mzimu wake wozichepetsa. Mzimu wake wowukira unali pankhondo ndi Mzimu ozichepetsa, omvera, wabwino wa Mwana wa Mulungu. Mzimu owukirawu udasefukira mwa mitundu ya anthu. Mu nsembe ya Yesu Khristu tikupasidwanso Mzimu wozichepetsawo. Chinsinsi chokhala ndi Mzimuwu ndikudziwa za momwe Atate ndi Mwana alili- uwu ndi moyo wosatha kumuziwa Atate ndi Mwana wake ndi kumwa madzi a moyo a kasupe wochokera ku mpando wa Mulungu ndi mwana wa Nkhosa.